

# YEHOVA-YIRE <sup>3</sup>



Zikomo inu, M'bale Borders.

Inu mukhoza kukhala. Kungokhala ndi chiyanjano ndi M'bale Harrel, wamkulu wa msonkhano, ndi kupeza kuti iye ndi mmishonare, ndipo ife tikukhala ngati tiri ndi zinthu zofanana. Iye akubwerera tsopano ku Gold Coast, Afrika. Ndipo ine ndikulinga kuti ndipite kumeneko chaka chino. Ife tinali kuyesetsa kuti tiyike chinachake pamodzi zokachezera ku Gold Coast titabwera kuchokera ku South Africa.

<sup>2</sup> Ndi kumene ife tinali, chimene ine ndikuganiza, umodzi wa misonkhano yayikulu kwambiri, mu tsiku langa, inali mu South Africa, pamene ife tinawona mbadwa za mabulangete sarte sauzande zikulandira Khristu pa nthawi imodzi. Ameni. Anawapempha iwo kuti aswere mafano awo pansi, kuti iwo ankatanthauza izo kwenikweni. Ndipo iwo anaswa mafano awo, ngati mkuntho wa fumbi ukubwera, ndipo anamulandira Khristu ngati Mpulumutsi wawo, pa msonkhano umodzi. Iwo anali ndi kutsatira kwabwino kumeneko, chotero iwo—iwo anawagwira iwo.

<sup>3</sup> Koma kuyitanira kuguwa kwakukulu kumene ine ndingakukumbukire, kumene Ambuye anatipatsa ife, kunali mu...kunali ku India, kumene tinali ndi pafupifupi faivi handirede sauzande mu msonkhano umodzi. Ndipo kumeneko ife—ife sitinathe kuyerekeza basi; basi monga momwe iwe ungathere kuwona, zinangokhala paliponse. Ndipo onse a iwo anamulandira Khristu ngati Mpulumutsi, koma panalibe chinthu chimodzi choti atsature nacho. Ndiye chotero, ndithudi, a—a Sikhs anatenga awo, Achijaini anatenga awo, ndi zina zotero. Ine ndikuganiza ambiri a iwo anabwerera mmbuyo, powona chinachake chimene Ambuye anachita ndi kuchitulutsa kumeneko.

<sup>4</sup> Utumiki wanga umene Ambuye anandipatsa ine, mu Amerika sukugwira ntchito kwambiri, anthu Achipentekoste okha. Mipingo yambiri ya mu Amerika ndi mipingo yaluntha kwambiri, ndipo iwo amakhulupirira kachikhulupiriro. Ndipo basi ndi kumene iwo amakhalako, iwe sungawasunthe iwo kwa izo.

<sup>5</sup> Koma pamene inu mumutenga mbadwa ndi kuyesera kumuza iye chinachake chokhudza kachikhulupiriro, iye samadziwa nkomwe dzanja lakumanja ndi lakumanzere. Kodi chimachita ubwino wanji kumupatsa iye ka tracki? Iye akuyenera *kuwona* chinachake. Ndipo pamene iye awona icho, ndiye amakhala wokhutitsidwa. Ndi kumuona sing'anga wake akuimirira ndi kutsutsa icho, ndi kuwona

Mzimu Woyera ukuyika icho pansi apo pomwe. Eya. Ndiye izo—izo zimawonetsera izo, amene ali Mulungu, ndiyeno izo zimakhazikitsa zimenezo.

Ndipo wokondwa kwambiri kukumana ndi M'bale Harrel! Ine ndinali. . .Ife tinkakamba za mbadwa za ku Afrika. Iye amayankhula za kuthandizira umodzi wa M'bale T. L. Osborn.

<sup>6</sup> Ambiri a inu mukumudziwa M'bale Osborn, ine ndikuganiza. Oh, apo pali wantchito wofunika wa Khristu, M'bale Osborn. Iye ndi mmodzi mwa azimzanga apamtima. Ine ndithudi ndiri ndi kulemekeza kwakuya mu mtima mwanga kwa M'bale Osborn, mmishonare wamkulu chotero. Ku a. . . Ine ndikukhulupirira iye wachita zochuluka ku minda ya umishonare kuposa aliynse padziko lapansi lero, amene ine ndikumudziwa, ndi—ndi M'bale Osborn. Wokoma kwambiri, mnyamata wabwino, ndipo ine ndithudi ndimamukonda M'bale ndi Mlongo Osborn.

<sup>7</sup> Iwo andiuzwa ine kuti Mayi Arganbright ali mu msonkhano usikuuno. Kodi inu mukubisala kwa ine, Mayi Arganbright? Ine ndithudi ndikuyamikira chipatso chanu chabwino. Ndipo nzosadabwitsa iye ndi dona wamng'ono wabwino chomwecho, iye wabwera kuchokera ku chigawo chino cha dziko kuno. Iye nthawizonse amayankhula za Grass Valley. Ndi angati amawadziwa Bambo ndi Mayi Arganbright, kuchokera ku Grass Valley? Chabwino, izo nzabwino. Inu muli pati, Mayi Arganbright? Ine sindinakuwoneni inu kwa nthawi yayitali, mmazemba. . .Ndi awo apo. Inde. Udalitsike mtima wake. Kwawo ndi kwathu kwachiwiri, mkazi wodabwitsa pomwe pano wochokera ku Grass Valley. Ndipo nthawizonse wakhala ali ndi kulemedwa kwa anthu awa. Ndipo Amayi Arganbright, ngati uno uli usiku wanu woyamba kuno, Ine ndinali uko kunkhalango ndikupemphera lero pamene inu munadzachezera mkazanga ndi iwo. Ndipo ndikupepesa kuti ine kunalibeko kuti ndikuwoneni inu, ndi kudzakumana ndi bwenzi lanu.

<sup>8</sup> Koma ndinena kuti ndawonapo chinachake chikuchitika pakati pa anthu anu kuno chimene sindinachiwonapo mu mzinda uliwonse waku Amerika kulikonse. Ine ndawawona Akhristu akuzindikira kuti alakwitsa, ku Mawu a Mulungu, ndipo akuimirira ndi kupempha chifundo. Eya. Izo zikumveka kwa ine ngati chitsitsimutso chikhoza kubwera kuno. Izo zingadzakhale zodabwitsa. Mochulukha momwe ine ndalalikira padziko lonse lapansi, ndipo makamaka mu Amerika, ine sindinawonapo nkale, magulu a Akhristu, pamene Mawu amabweretsedwa, kuwonetsera Mawu, iwo amaimirira ndi kumati (amachitira umboni) iwo amalakwitsa. Osati zokhazo, koma atumiki ndi iwo. Tsopano, kumeneko ndi kuwona mtima. Ine ndikuzikonda zimenezo.

<sup>9</sup> Mlongo Arganbright, popeza iwo anakuimiritsani inu,

ndimuchititsa manyazi mkazi wanga. Iye ndi munthu wamanyazi kwambiri padziko lapansi. Koma iye wakhala pano usikuuno. Wokonedwa, ndikukhulupirira iwe ukathana nane ine chifukwa cha ichi, koma ine ndimufunsa mkazi wanga kuti ayimirire. Mkazi wokoma kwambiri mdziko lonse, kwa ine. [Osonkhana akuwombera mmanja—Mkonzi].

10 Mtsikana wanga, mwana wanga wamkazi, mwana wanga wamkulu, Rebekah. Tsopano, wokonedwa, ine ndikudziwa kuti wapsya ndi dzuwa, koma ine ndikufuna kuti iwe uyimirire, mulimonse. Chabwino, Rebekah. Ameneyo ndi mwana wanga wamkazi, Rebekah. [Osonkhana akuwombera mmanja—Mkonzi]. Zikomo inu. Zikomo inu.

11 M'bale Jewel Rose, ndi angati amamudziwa iye? Usiku wina iye anamuza mkazi wanga kuti abwere ku nsanja kumene ine ndinali, iwo utayamba kale. Iye anakhala ngati akomoke. Iye amangomuzemba iye kulikonse kumene angamuwone iye. Iye amatalikira kumene iye ali, chifukwa amawopa kuti amuyitaniranso ku nsanja.

12 Ine ndinamuza iye, “Usiku wina ndidzakupangitsa iwe kuyimirira ndi kuyankhula kwa kanthawi pang'ono kwa ife.”

13 Iye anati, “Udzakonzekere chidebe chamadzi, chifukwa ine ndidzakomoka.”

14 Iye ndi munthu wokonedwa kwambiri, mkazi wanga. Ngati pali kuyamikira kulikonse koti kuperekedwe ku banja la a Branham, mulole iko kupite kwa iye. Iye ndi amene amayima pakati pa ine ndi anthu. Ndipo zinthu zonse zimene zimachitidwa molondola, iyeyo ndi amene amachita izo.

15 Ine ndikuyembekezera kuti mnyamata aliyense pano, iye akamadzakwatira, iye adzapeza mkazi, ndipo mudzakhala okondwa limodzi monga mkazi wanga ndi ine tachitira zaka twente-thuu izi zimene ife takhala tiri m'banja.

16 “Iye amene wapeza mkazi, wapeza chinthu chabwino.” Monga Solomoni anati, “Mkazi wabwino ndi ngale mu korona wa mwamuna. Wosalungamayo ndi madzi mmagazi ake.” Ndipo moyenda magazi mwake ndi moyo wake. Chotero, wosalungama ndi chinthu choyipa kwambiri chimene iye angachitenge. Ndipo wolungamayo ndi chinthu chabwino kwambiri chimene iye angachitenge, kunja kwa chipulumutso. Ngati Mulungu akanamupatsa mwamuna chinthu chabwino kuposa mkazi, Iye akanampatsa iye chimenecho, chifukwa Mulungu amangowapatsa ana Ake zinthu zabwino. Ndipo Iye anampatsa iye mkazi, ndipo ndine woyamikira chifukwa cha zimenezo.

17 Ndipo kuwawona akazi, pamene ine ndinkakhala ngati ndikudula usiku wina, ndi Lemba pa momwe akazi Achipentekoste awa akuvalira, kuvala tsitsi lawo, ndi kumapita.

Inu mukuti, “Izo sizimapanga kusiyana kulikonse.” Izo ndithudi zimatero!

<sup>18</sup> Ine ndikufuna ndikufunsi inu chinachake. M’bale Harrel ali pano, mmishonare.

<sup>19</sup> Ku Durban, South Africa, kunali akazi atakhala pamenepo amaliseche momwe iwo anabwerera pa dziko lapansi; analibe konse msoko umodzi wa zovala, anangokhala ndi korona, wa pafupifupi foro-, ma inchi sikisi patsogolo pawo. Ndipo atayima pamenepo amaliseche momwe iwo anakhalira, ndipo atayima panso chozizwitsa chachikulu ichi chitachitika pa nsanja. Ndipo munali mu gulu limenero, munali pafupifupi Achimuhamedi teni sauzande (pa nthawi imodzi) anamulandira Khristu mu msonkhano womwewo. Ndipo kenako mmenemo pamene... Akazi awa, ataimirira ndi amuna awa, anamulandira Khristu.

<sup>20</sup> Ndipo M’bale Bosworth anati, “M’bale Branham, ine ndikukhulupirira inu mukuyenera kupanga kuyitana kumeneko kachiwiri. Ine ndikukhulupirira iwo amatanthauza machiritso ‘athupi.’”

<sup>21</sup> Ine ndinati, ndithudi, otanthauzira fifitini osiyanasiyana. Inu mukudziwa, izo zimatengera...Iwe umayenera kulemba chimene wanena, nthawi iwo...Iwe ukati, “Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu, anabwera kudzapulumutsa ochimwa.” Ndipo uyu amati “blu, blu, blu, blu,” ndipo uyu amati “nic, nic, nic, nic,” ndizo “Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu.”

<sup>22</sup> Inu mukudziwa, ine—ine ndinkakonda kuwamva anthu akuyankhula mmalirime, ndipo ine ndinaganiza, “Mai, izo sizingakhale zolondola.” Koma Baibulo linati, “Sipangakhale phokoso popanda tanthauzo lake.” Palibepo. Pamene ine ndinamva izo, ena a iwo amalira ngati mbalame, ena amalira ngati nsikidzi, ndi chirichonse. Koma izo zimatanthauza tanthauzo kwa iwo, izo, phokoso lirilonse limakhala tanthauzo.

<sup>23</sup> Ndipo pamene izo zidutsa kachiwiri, ndipo ine ndimati, “Chabwino, ndiye mulole iwo tsopano amene akudziwa kuti izi si kwenikweni machiritso ‘athupi,’ ndi kumalandira Khristu ngati Mpulumutsi, Kumwamba koti tidzapitako, inu mukhulupirire mwa Mwana wa Mulungu, mumulandire Iye ngati Mpulumutsi wanu, muswe mafano anuwo panso!” Ndipo iwo amawatayira iwo panso. Ndipo ine nkuti, “Apo pomwe tsopano, kwezerani mmwamba manja anu kwa Mulungu ameneyo, ndipo mumpatse Iye matamando. Iye akupatsani inu Mzimu Woyera!”

<sup>24</sup> Ndipo nditayima pa bwalo limenero, ine ndinawona akazi amene anali maliseche kwathunthu; ndipo mwamsanga pamene Khristu anawakantha iwo, iwo amachoka pa bwalolo atapsyatira manja awo. Ndipo pamene iwe umadzawawonanso iwo kachiwiri, iwo anali atavala zovala.

25 Tsopano, ngati Khristu angamupangitse wachikunja (wamaliseche) kuzindikira kuti iye akulakwitsa, pokhala wamaliseche, ndiyeno akazi amene amadzinenera kuti ndi Akhristu ndipo chaka chirichonse amavula mochuluka, sindingathe kuzimvetsa izo. Pali chinachake cholakwika penapake.

26 Wachikunja weniweni, atangoyima pamenepo, wobadwa mdziko lino ndipo wosadziwa konse kuti iye ndi wamaliseche, iye sakudziwa kuti ali maliseche. Koma mulole Khristu abwere pamaso pake, iye amazindikira kuti ali maliseche, mochuluka momwe iye angayese kudziphimba yekha mochuluka momwe iye angathere, kupinda manja ake ndi kuchokapo. Patapita masiku awiri kapena atatu, mudzamupezanso iye, atavala.

27 Tsopano pali chinachake cholakwika penapake, ndipo ine ndikutsimikiza kuti sichiri ndi Khristu. Oh, ine ndikuganiza kuti Mawu ndi angwiwo!

28 Ine ndimangowukonda ulendo wa Abrahamu. Sichoncho inu? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Ine ndikukhala nawo iwo nthawi yaitali, ine ndikuyembekeza kuti ndifika ku *Yehova-Yire* usikuuno. Ine ndinatenga mutuwo, mausiku atatu kapena anayi apitawo, ndipo sindinafike kwa iwo.

29 Koma chaka chimodzi kwathu ndinatenga phunziro, ndikulalikira za Yobu. Chabwino, pafupifupi chaka ine ndinali mu Bukhu la Yobu, Lamlungu lirilonse ndi Lachitatu, pa Yobu. Ndipo potsiriza ndinamudzutsa iye mpaka iye anadzakhala pa mulu wa phulusa. Ine ndinamuika iye pamenepo pafupifupi masabata atatu kapena anayi. Ndipo mmodzi—mlongo mmodzi wofunika wolimba mtima mokwanira anandilembera ine, anati, “M’bale Branham, kodi inu mudzamuchotsapo liti Yobu pa mulu wa phulusa?”

30 Chabwino, ndikulingalira kuti mukudabwa kuti ndi liti limene ndidzamutenge Abrahamu kuti akamuwone *Yehova-Yire*.

31 Koma ndinali ndi mfundo. Abrahamu... Kapena, Yobu atakhala pamenepo pa mulu wa phulusa, Elihu akuyankhula: Mulungu akumuyesa woyerayo. Ndinazibweretsa izo zonse mmenemo, mpaka ine ndinafika pamene ine ndikanakhoza kupanga kuwomberako, ndinakonzekeretsa chirichonse. Kenako Ambuye anabwera pamenepo mu kamvuluvulu uyu, ndipo mphezi zinayamba kung’anima, ndipo mabingu anabangula. Ndipo Mzimu wa Mulungu unadza pa mneneri, iye anayima pa mapazi ake, anati, “Ndikudziwa Muwomboli wanga ali moyo;” penyani “Muwomboli.” “Ndipo mmasiku otsiriza Iye adzayima pa dziko lapansi. Ndipo ngakhale mphutsi za khungu zitawononga thupi ili, komabe mu thupi langa ine ndidzamuwona Mulungu; Amene ndidzamuwona ndekha, maso anga adzamuwona, ndipo osati wina.” Oh, ndi phunziro bwanji

pamenepo! Kuti izo zilowe mkati, izo zinatenga kanthawi kuti anthu onse akhazikike, Mzimu molondola basi, kenako nkulondoloza izo. Ndipo kenako guwalo linafoledwa ndipo linadzazidwa ndi anthu, akulapa.

<sup>32</sup> Basi ngati iwe ukutsogozedwa ndi Mzimu, ungotenga nthawi yako kufikira utalunjikamo. Ukapanda kutero, umawombera pamwamba kwambiri kapena umawombera motambalala kwambiri, kapena chinachake. Tiyeni tizipange izo molunjika, Baibulo! Ine ndikukhulupirira kuti Mulungu amafuna kuti ife tizilunjika. Mzimu Woyera unalunjikizana ndi atumwi, kapena iwo analunjikizana ndi Mzimu Woyera, kani. Ndipo ine ndikukhulupirira ife tikhocha kuchita chinthu chomwecho, ndi Mawu omwewo. Iwo agunda chandamale! Ndipo ngati izo zinagunda izo nthawi ina, pakati penipeni, izo zikhocha kugunda izo kachiwiri! Koma mukuyenera kulunjika! Mungowonetsetsa kuti kupuma kwanu, kukoka kwanu, zonse ziri bwinobwino. Ine ndimawombera chandamale; ine ndikudziwa chimene izo ziri, kudziyala mu mpikisano, ndi mfuti imene ingalunjike.

<sup>33</sup> Nthawi ina ine ndinatumiza mtundu wa yaying'ono ya sevente-faivi ndinaibweza ku Winchester Company, tsiku lina. Ndipo ine sindimatha kuipangitsa iyo kuti imenye pafupifupi firii... kapena korta ya inchi, pa mayadi fifite. Ndipo Winchester Company inabwezeranso iyo kwa ine, anati, "Abusa Branham, mfuti imeneyo inangopangidwira kuti—kuti izingowombera pa gulu la faivi, inchi pa mayadi twente-faivi." Tsopano imeneyo inali kampani imene inapanga iyo. Ine ndikudziwa mosiyana. Ine ndinangowombera, pa mzere, molondola, kanaini molunjika, timbendera, pa mayadi fifite, ndi iyo. Chotero ine ndinadziwa kuti iyo imalunjika. Chotero ine ndinangopitirira kumasewera nayo iyo, ndi kumasewera nayo iyo, mpaka ine ndinaipangitsa iyo kuti ilondolere kachiwiri.

<sup>34</sup> Tsopano, chinthu chomwecho chimachitika ndi Mawu a Mulungu. Zinthu zimenezo zimene atumwi aja anachita, zinthu zimenezo zimene Khristu analonjeza, ife tikuyenera kulunjikizana ndi Mawu, ndi Mzimu. Ngati izo zinachitika nthawi imodzi, izo zidzachita izo kenanso, chifukwa Iwo ndi Mulungu. Ndipo Mulungu ndi Mawu, ndipo Iye sangalephere.

<sup>35</sup> Ngati itakhala yosasuntha, mfuti itakhala yomasuka pang'ono mbali *iyi* pa pamkono, yomasuka pang'ono kapena yothina kwambiri, chirichonse chimene chimamanga iyo, inu mukhoza kuyika kulemera kwa chala chanu pa mfutiyo, ndipo (iyo nkumawombera bwino bwino) kulemera kwa chala chanu kungawuponyere iwo kumbali. Inu muyenera kukhala ndi chirichonse chiri changwiro.

<sup>36</sup> Umo ndi momwe inu mukuyenera kuchitira mu Chikhristu, kuti muwapangitse Mawu, kuwapanga iwo kuti awonetsere ndi kuchita molondola, inueni ndi Mawu ndipo ndi Mulungu,

izo zikuyenera kukhala zangwiro, ndipo zikatero iyo idzalunjika. Zikuyenera kutero! Chotero ndiye, mu kulalikira, inu mukuyenera kuwumverera Mzimu mwabwino basi, kenako nkulunjika; kutali iyo idzapita, iyo idzalondolera ku chandamale.

<sup>37</sup> Ndiye anthu atakhala mozungulira, nthawi zambiri anthu amati, “M’bale Branham, ine sindimamva za misonkhano yanu.”

<sup>38</sup> Ine ndiribe zofalitsira monga abale ena amachitira. Iwo ali ndi magazini, iwo ali—ali ndi wayilesi, televizioni. Ine ndimangodutsamo ndi kuyesera kuti ndiwayimire Ambuye Yesu. Anthu amawona zimenezo, amakhulupirira izo, iwo amakhala bwino. Mulungu akudziwa zimenezo, ndizo zonse zimene ziri zofunikira. Mukuona? Ife sititero, ife sitiri... Sipadzakhala mbiriyakale yolembedwa. Musadandaule ndi zimenezo. Sipadzakhala nthawi yolemba mbiriyakale. Ine ndikukhulupirira kuti Yesu akubwera. Izo, ine ndikukhulupirira zimenezo. Ndipo ine ndikufuna ndizikhala moyo lero ngati kuti Iye abwera lero kapena mawa. Osati masukulu aakulu kwambiri, ndi zina zotero. Kodi ife timachitiranji zinthu zimenezo, ndipo kenako nkumalalikira kuti Yesu akubwera? Bwanji, ntchito zathu zomwe zimachitira umboni motitsutsa ife. Uko nkulondola. Yesu akubwera, tiyeni tikhale, tiwukonzekeretse mpingo kukonzekera izo! Tiyeni tikonzekere. Oh, momwe ine ndimamukondera Iye!

<sup>39</sup> Tiyeni tiweramitse mitu yathu tsopano ku mawu a pemphero. Oh, momwe ine ndimakondera kuwawona anthu pamene iwo molemekeza akuweramitsa mitu yawo. Tsopano tiyeni tingokhala chete kwa kanthawi pang’ono, ndipo tiphunzire. Tsopano ife tikufuna kuti titenge nthawi yathu. Mawa ndi Lamlungu, la sabata, tsiku la sabata la Chikristu. Ndipo sindikufuna inu mudzachedwe ku Sande sukulu, ngakhale ife sitikufuna kuti tizithamangitse zinthu izi.

<sup>40</sup> Taganizani tsopano, “Ambuye, kodi chokhumba changa mu mtima mwanga usikuuno chikugwirizana ndi chifuniro Chanu?” Ngati icho chiri, ndiye inu muganizire za icho. Ndiye ngati inu mukuganizira za icho, chokhumba chanu, ndipo muchifufuze icho ndi programu ya Mulungu, ngati icho chikuwoneka kuti ndi cholondola ndi programu ya Mulungu, ndiye ine ndikufuna inu mukweze dzanja lanu kwa Mulungu, ndi kuti, “Mulungu, mundikumbukire ine, ichi ndi chimene ine ndikuchisowa.” Mungoganizira molimbika kwenikweni. Mulungu akudalitseni inu. Zabwino. Ambuye akudalitseni inu. Izo nzabwino. Mungopitirira kukweza dzanja lanu. Iye amawona zonse. Iye amadziwa zinthu zonse. Izo nzabwino. Mulungu akudalitseni inu. Ameni. Ambuye adalitse. Izo nzabwino. Mungopitirira kuganiza, kukweza dzanja lanu mmwamba. Tsopano ine ndikuwona dzanja lirilonse pamene ilo likukwera mmwamba. Chabwino. Ziri bwino.

41 Atate Akumwamba, ife tsopano tikubwera, tikuyandikira kachiwiri mu Dzina lokwanira-zonse ilo la Ambuye Yesu, mpaka ku Mpandowachifumu wa Chifundo. Monga wandakatulo ananena, “Ndiloleni ine pa Mpandowachifumu wa Chifundo, ndikapeze kumasulidwa kokoma.” Ndipo, Mulungu, mitima yawo yaledwa ndi chinachake. Ndipo aloleni iwo tsopano, pa Mpandowachifumu wa Chifundo, akapeze thandizo limene Mulungu akulipereka kwa iwo, Msing’anga wamkulu, ndi chikhulupiriro cha chimene iwo akuchisowa.

42 Ndakwezera manja anga awiri onse mmwamba. Ine ndiri ndi zosowa. Mundikumbukire ine, Ambuye.

43 Akumbukireni anthu onsewa pano amene mipango iyi ikuyayimira. Oh, momwe maumboni abwerera chifukwa cha zinthu izi. Kulemekeza. Kutali uko kudutsa mapiri amchenga awa kuno, kwina kwake, amayi odwala, azibambo, makanda, anthu mchipatala, adadi okalamba akhungu atakhala kumbuyo pa kachipinda kakang’ono ndi ndodo yoyera mdzanja lawo, akuyembekezera kubwerera kwa mipango iyi. Mulungu, tichitireni chifundo. Perekani, Ambuye, kuti pa aliynse amene iyo ikaikidwepo, mulole mdani akataye mphamvu yake ndi nyonga, mulole iwo apite ndi kukachiritsidwa. Apa pali wina walembedwa apa, “khansa.” Mulole mdierekezi ameneyo awamasule iwo, Ambuye. Mulole Mzimu Woyera, pamene Mulungu akuyang’ana pansu kupyolera mu Magazi a Mwana Wake Yemwe amene anafera cholinga ichi, mulole chitetezero chachikulu chikhale chokwanira usikuuno, ndipo chikhulupiriro chikhale chikusefukira mochuluka pa iwo, ndipo iwo, kapena, mochuluka, kuti iwo akakhoze kulandira machiritso awo. Perekani izi, Ambuye.

44 Adalitseni Mawu Anu tsopano. Mthandizeni wantchito Wanu, tidzozzeni ife ku utumiki. Dzodzani mtima uliwonse umene ukumva. Ndipo ife tingoyankhula tsopano, Atate. Inu mutiuze ife zoti tinene, ndi kutiuza zoti tichite. Ife tikuyembekezera Inu kuti mukhale nafe mu msonkhano.

45 Zikomo Inu chifukwa cha nyimbo zabwino usikuuno, nyimbo zokongola zimenezo. Mnyamata uyu kumbuyo kuno, M’bale Heimer, anangoyimba nyimbo yopambana ija, *Waku Galileya*. Mulole Mlendo waku Galileya ameneyo adzalowe tsopano usikuuno. Mulole ife timve liwu Lake likunena kwa malingaliro ovutika, monga Iye anachitira pa madzi ovuta, “Bata, pakhale bata.” Ndipo mulole mtima uliwonse wosautsika uchrirtsidwe. Ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amen.

*Ndipo iye anatcha dzina la malowo Yehova-yire: monga kwalembedwa, Paphiri la AMBUE chidzawoneka.*

46 Tsopano ife tikufuna kuti tiyambe ndi munthu wamkulu uyu. Ndipo mawa . . . Tsopano, Ambuye akalola, ife tiyesetsa kuti



tifike kumapeto zokhudza Abrahamu usikuuno. Ndipo mawa, mwinamwake mutu pa machiritso Auzimu.

<sup>47</sup> Ambuye wakhala wabwino kwa ife pano. Ife takhala tikumva maumboni a zinthu zimene zachitika. Ndipo wokondwa kwambiri! Ndipo ife tinali ndi usiku umodzi, mzere wathunthu wa pemphero, kapena tinawayitana iwo. Ndipo panalibe wina wofooka amene ife tinamuwona mchipindamo, chikuku, paliponse, koma amene anadzuka, akuyenda pozungulira, akupita.

<sup>48</sup> Ndipo tsopano usiku uliwonse Mzimu Woyera umabwera mu Kukhalapo Kwake kopambana, kwaulemu, ndipo umapita kudutsa mwa omvetsera, akudziwonetsera Yekha, kuti Iye ali pano. Ndiye, ife tikuyenera kumukhulupirira Iye. Mwaona, Iye akufuna kuti inu mumukhulupirire Iye. Ulemu waukulu kwambiri umene mungapereke kwa Mulungu ndi kumukhulupirira Iye. Inu mukuyenera kukhulupirira. “Iye amene abwera kwa Mulungu akuyenera kukhulupirira kuti Iye ali.” Ndipo tsopano mukhulupirireni Iye!

<sup>49</sup> Ndipo pamene ine ndikumutenga Abrahamu, ulendo, ndi chifukwa chakuti ine ndikuyesetsa kumanga chikhulupiriro kufika pachimake chachikulu, kuwalola anthu kuti awone chimene iwo ali.

<sup>50</sup> Limenero ndiro vutolo. Ine ndimapeza magulu awiri a anthu, pamene ndikuyenda. Mmodzi wa iwo ndi wachipentekoste, winayo ndi wachikhazikitso. Tsopano, wachikhazikitso mwapamalo amadziwa kumene iwo ali, chimene iwo ali, koma iwo alibe chikhulupiriro chirichonse ndi izo. Achipentekoste amakhala ndi chikhulupiriro, koma samadziwa kuti iwo ndi ndani. Tsopano, ziri ngati munthu amene ali ndi ndalama ku banki, koma iye samadziwa momwe angalembere cheke; ndipo winayo akhoza kulemba cheke, ndipo alibe ndalama ku banki. Ngati inu mutangowayika iwo pamodzi, chinachake chingachitike. Inu mutangokhala konse ndi chikhulupiriro cha chipentekoste ndi chiphunzitso cha chikhazikitso, ngati mutangokhala konse...kapena kukhala ndi chiphunzitso chachikhazikitso ndi chikhulupiriro cha chipentekoste, chinachake chikhoza kuchitika. Uko nkulondola.

<sup>51</sup> Tsopano, momwe ine ndikanafunira kuti ndipereke umboni pano, pamene ine ndinawona, sukulu ya Chilutera, foro handirede analandira Ubatizo wa Mzimu Woyera ndikuyankhula ndi iwo pa izo. Oh, mai, anali mawonekedwe a ulemelero, kuwadziwitsa iwo zimenezo. Iwo siali, chifukwa iwo ndi Achilutera, iwo sawerengedwa kunj.

<sup>52</sup> Palibe chotsutsa Achilutera, Abaptisti, Amethodisti, chirichonse chimene inu muli, Chikatolika. Ine sindikutsutsana nazo zinthu zimenezo. Sindikutsutsana nawo anthu amenewo. Ndi kachitidwe kamene kamawagwira iwo, ndi chimene

ndimayankhula motsutsana nacho. Palibe chotsutsa munthu payekha, iwo onse ndi anthu amene Khristu anawafera; Mkatolika, Myuda, chirichonse chimene iye angakhale. Ndi kachitidweko. Monga Achimuhamedi, Achisikh, Jain, kapena chirichonse chimene chingakhale, ndi kachitidweko. Buddha ndi kachitidwe, mwaona. Osati anthuwo amene—amene amapembedza Buddha; ndi kachitidwe kamene kamawachotsapo iwo.

<sup>53</sup> Ndi chinthu chomwecho. Yesu sankatsutsana ndi anthu. Iye anawafera iwo. Koma kachitidwe kameneko kamene kankamuyika Iye kutali, kuwachotsa iwo kutali ndi Iye. Ndicho chinthucho tsopano.

<sup>54</sup> Tsopano ine ndinaganiza, pomutenga Abrahamu, podziwa kuti izo zinali kwa Abrahamu lonjezo linaperekedwa, ndipo Mbewu ya Abrahamu ya pambuyo pa iye. Tsopano tiyeni tibwerere mmbuyo pang'ono pokha ndi kukapeza maziko, ndi kubwera usikuuno molunjika ku mutu tsopano kwa kanthawi pang'ono.

<sup>55</sup> Ndipo makhadi apemphero aperekedwa kwa aliyense amene akufuna kuti apemphereredwe. Ndipo ife, ngati simulandira iwo onse usikuuno, tidzalandira iwo mawa. Ndipo aliyense amene akufuna kuti apemphereredwe akuyenera kukhala ndi khadi la pemphero. Ndipo mudzakhale pano hafu pasti wani mawa, kuti mudzatenge khadi lanu la pemphero, chifukwa ife tikufuna kuti tidzayambe msonkhano pamenepo. Ndipo ife tidzapempherera munthu aliyense amene adzakhale ndi khadi la pemphero mawa. Ife takhala tikuyesetsa, kudutsa mausiku, kuti tipeze iwo amene alibe makhadi apemphero, kuchitira kuti iwo amene ali ndi makhadi a pemphero akhale ndi mwayi wokhala mu mzere wa pemphero. Ndipo ena amaitanidwa kumeneko, opanda makhadi a pemphero. Izo zimafikira kuwiri konse, mbali ziwiri zonse. Khadi la pemphero silitanthauza kanthu. Koma inu mumamupatsa munthu khadi la pemphero, pamakhala pafupifupi forte peresenti ochiritsidwa pomwe apo, ndi inuyo amene mumaganiza kuti iye akudutsa pamzere; chinachake chimene iye akhoza kuchigwira, chinachake chimene iye akhoza kumachiyang'ana, kapena chinachake. Ndipo a—mnyamatayo adzakhala akupereka makhadi apemphero mawa hafu pasti wani, chotero iwo akhoza kukhala atachoka pofika thuu koloko, chotero ena onse—zochitika za tsiku iwo amapeza.

<sup>56</sup> Ndipo inu amene mukufuna chithunzi, bukhu, kapena tepi, mukuyenera kukhala nazo usikuuno. Palibe kugulitsa Lamlungu; ife sitimaloleza konse zimenezo, kugulitsa izo. Ife timalemekeza Lamlungu, sitimagulitsa konse Lamlungu. Ndipo mabukhu awa ndi zinthu, iwo si kanthu kwa ine, iwo ndi mabukhu amene anthu alemba okhudza utumiki wanga. Zithunzi zimene a American Photographer Association anajambula chithunzichi, ndipo icho ndi cha Douglas Studio,

ndi chotetezedwa. Bukhuli ndi la M'bale Gordon Lindsay ndi Chaplain Julius Stadskev. Ife timawagula iwo ndi kuwabweretsa iwo ku msonkhano, ndi kumagulitsa iwo pafupifupi mtengo umene ife tinawapezera iwo, ndipo osapindulapo pa iwo. Ndipo ife nthawizonse timanena izi, ngati wina . . . Ndawauzapo anthu amene amagulitsa mabukhu, “Ngati mwamuna kapena mkazi abwera uko, munthu wosauka, alibe ndalama zogulira bukhu limenero; liperekeni ilo kwa iwo, mulimonse. Ndipo ife tidza . . . Ine ndidzawonetsetsa kuti izo zikusamaliridwa.” Ndipo ngati inu munagula bukhulo ndipo silikuyenera mtengo umene ilo likuyenera kukhalira, libwezeni ilo. Sipadzakhala kubweza kumodzi kopanda kanthu koma kubweza ndalama zanu, mwaona. Ndi chinachake basi chothandizira chikhulupiriro chanu. Ndizo zonse zimene ife tikuyesetsa kuti tichite izo, kapena ife sitingalole kuti izo zikhale pano. Ndizo kulondola ndendende. Chotero tsopano usikuuno, kumbukirani, iwo adzakhala ali pa choyikapo mabukhu. Mzanga wabwino wa ine, Bambo ndi Mayi Wood. Ndikanakonda ndikanakhala ndi nthawi yoti ndikuuzeni inu umboni wawo, wa momwe mwana wawo anachiritsidwira ku poliyo. Ndi zinthu zina zambiri zimene—zimene zachitika, za anthu amene ali pano mu msonkhano.

<sup>57</sup> Tsopano tiyeni tiyike maziko a Abrahamu. Poyamba, Mulungu anakumana ndi Abrahamu, mopanda mangawa, pangano limene Iye anapangana ndi Abrahamu. Popanda chirichonse nkomse; Abrahamu analibe chochita koma kukhulupirira Mulungu. Panganoli linali mwangwiro la chisomo, ndiponso lopanda mangawa. Osati “ngati ukadzatere.” Mulungu anati, “Ine ndatere!” Ndipo tsopano munthu aliyense . . .

<sup>58</sup> Kumbukirani, Mbewu yonse ya Abrahamu imene inabwerapo kwa Mulungu, imabwera mwanjira yomweyo. Osati kalikonse kamene mukanachita! Inu simungathe kudzipulumutsa nokha kuposa momwe mukanatengera zingwe za nsapato zanu ndi kulumphira pa mwezi. Inu simungathe kudzipulumutsa nokha. Palibe munthu amene anayamba wamufunafunapo Mulungu; ndi Mulungu amamufunafuna munthu. “Inu simunandisankhe Ine,” Yesu anati, “Ine ndinakusankhani inu.”

<sup>59</sup> Choyamba, tsopano, kodi inu mungapite kunja kuno ndi kukaiwuzana nkhumba kuti iyo ikulakwitsa, kudya matope? Iyo idzakuzani inu kuti samala zako. Koma payenera kutengera chinachake chimene chingasinthe chikhaliidwe chake, kuti chimupangitse iyo kuzindikira kuti iye akulakwitsa. Chinachake chikuyenera kuchitika kwa nkumbayo, poyamba.

<sup>60</sup> Ndi chifukwa chake kuti otchedwa Akhristu nthawi zambiri amadzigudubuzana mmatope, kubwerera mu tchimo, ndi chifukwa . . . Inu mukhoza kuyisambitsa nkhumba, ndi kuipenta

zikhadabo zake, kuyika zopaka mmilomo. Izo, izo nzolakwika, chirichonse chimene icho chiri. Zopaka mmilomo, sichoncho, kapena chinachake? Ine ndimazitenga zimenezo, zinthu zonsezo, ndimazisakaniza. Inu mukudziwa chimene izo ziri, chonchobe. Inu muyiyike nkumba yakale pa zopaka mmilomo zina ndi—ndi, inu mukudziwa, kuchita ntchito zina zonse pa iyo, ndipo iyo idzapita molunjika ku matope, ndi kumatope kachiwiri. Chifukwa chiyani? Iyo ndi nkumba, kuyamba ndi kuyamba. Njira yokhayo imene inu mungayipange kukhala yosinthika, ndi kusintha chikhalidwe chake.

<sup>61</sup> Ndiyo njira yokhayo imene mwamuna kapena mkazi angathe kugwirizana ndi Mulungu, ndi kusintha chikhalidwe, kuyetsa, kufa ku tchimo la munthu wakale, ndi kubadwanso mwatsopano mwa Mzimu wa Mulungu. Ndipo, izo ndi, Khristu ndi Mzimu wa Mulungu, ndipo Khristu ndi Mawu. Ndiye iwo umachitira umboni ndi Mawu. Ndiyo njira yokhayo imene iwo angachitire izo.

<sup>62</sup> Tsopano, Abrahamu ankafunafuna Mzinda Umene Wowumanga ndi Wowupanga anali Mulungu. Ndipo lero ndife amwendamnjira, alendo, tikufunafuna Mzinda Umene Wowumanga ndi Wowupanga ndi Mulungu. Penyani! Abrahamu, iye asanadziwe nkomwe, munali chinachake chonga ngati kununkhiza mwa iye, kuti iye ankayang'ana pa Mzindawo.

<sup>63</sup> Lero, ndikudutsa kumusi ndi mkazi wanga, ine ndinali kuyankhula, “Malo aang’ono okonedwa apa ali pa phiri, mwinamwake zaka firii handirede zapitazo; thengo lokongola, mitengo yayitali kwambiri. Munthu anadzabwera, iwo anadzaidula iyo, kuyipitsa mitsinje. Iwo akanakhala malo okongola kukhala kuno.” Eya, koma inu mwaona, iye anamanga manyumba. Kenako iwo amayamba kuchulukana. Tchimo ndi chiwawa zinayamba kulowamo. Hollywood inasunthira pafupi ndi iye, zinabweretsedwamo ndi kanema, ndi televizion. Mwa . . . Ndipo tsopano ndi woyipitsidwa, wochimwa, mzinda uliwonse!

<sup>64</sup> Ndipo ndithudi, monga anthu, chinachake mwa iwo chimakonda kukhalira limodzi, kwa woyandikana naye, ndi kukhala olungama. Ndithudi ulipo Mzinda kwinakwake! Chakuya chimayitanira ku Chakuya kachiwiri!

<sup>65</sup> Ndipo Abrahamu anawona mizinda ya tsiku lake, Uri waku Kaldeya. Ndipo iye ankadziwa zimenezo chifukwa munali chinachake mwa iye chikuyitanira, uko kunali Mzinda umene unali wosiyana, Umene Wowumanga ndi Wowupanga anali Mulungu. Ndipo Mulungu anawona kuti mwa Abrahamu, anamuwuzwa iye, “Dzipatule wekha tsopano, tulukako.”

<sup>66</sup> Tsopano, Abrahamu, chinthu chimodzi chimene ine ndikufuna kuti inu muchizindikire, iye anamvera Mawu a Mulungu molondola.

67 Nthawizonse muzikumbukira zimenezo! Ndiwo Uthenga wanga. Inu mukuyenera kumvera Mawu. Ndipo kudziwa chirichonse chosiyana ndi Iwo, chisiyeni icho chokha. Icho chikhoza kumawoneka bwino, koma musamaganize motsutsana ndi Mawu a Mulungu.

68 Ndicho chinthu choyambirira chimene Satana anachita, chinali kukamba motsutsa Mawu a Mulungu, kwa Eva. Ndipo iye sanawakaikire konse Iwo. Iye anangowalingalira. Satana anawalingalira Iwo.

69 Ndipo umo ndi momwe iwo akumachitira lero. “Kodi sizikumveka zanzeru kuti ife tizichita *izi*? Kodi sizikumveka zanzeru?” Ngati izo ziri zotsutsana ndi Mawu a Mulungu, zisiyeni izo zokha! Ndi liwu la Satana.

70 Muwalole Mawu, ngati Mawu ali mwa inu. . . “Ngati inu mudzakhala mwa Ine, ndi Mawu Anga mwa inu, mudzapemphe chimene mukuchifuna.” Mzimu Woyera! “Inu mukadzakhala mwa Ine, Mawu Anga mwa inu,” amenewo ndi Mawu atasandulika thupi, “mudzapemphe chimene mukufuna ndipo chidzachtidwa.” Ndiyo njira yake. Chotsani tizikhulupiriro tonse, zinthu zonse, ndipo mugwiritsitse ku Mawu chifukwa ndi Khristu. Zindikirani, ndiye izo zidzaziwonetsera zokha.

71 Winawake anati, “M’bale Branham, inu mumadziwa bwanji zinthu zimenezo. Motani?”

72 Izi zimene mumaziwona pano mu msonkhano ndi zinthu zazing’ono. Aliyense amene amaitsatira misonkhano kuno, akudziwa. Mzimu Woyera umawulula zinthu zimene zimabwera masabata ndi miyezi pakati pa nthawi. Ndipo mumufunse aliyense, “Kodi izo zinayamba zalepherapo nthawi imodzi?” Izo sizingalephere, mwaona. “Inu mumadziwa bwanji izo?” Chifukwa ndi lonjezo la Mawu, ndipo ora lafika. Izo ziyenera kuchitika. Tsopano, ine sindikudziwa, pakhoza kukhala ochepa kwambiri, gulu lochepa lidzakhulupirira izo, koma izo zikuyenera kupita mofanana basi. Ndipo kodi inu munayamba mwazindikirapo, izo zimapita pamwamba pa mutu wa anthu, ndipo izo zinapita ndipo zinachitika iwo asanazindikire izo. Nthawizonse mwanjira imeneyo.

73 Kwa inu anthu Achikatolika, inu mukudziwa chimene mpingo wanu unachita? Chifukwa Joan waku Arc anali a—woyera weniweni wa Mulungu, anachita zozizwitisa za Mulungu, analoseredwa ndi Mulungu, ndipo inu munamutcha iye mfiti, ndipo munamuwotcha iye pa nkhu; ndi iye akukuwa kufuna chifundo, ndipo inu munamuwotcha iye pa nkhu. Mahandirede a zaka mtsogolo, inu munadzazindikira kuti inu munalakwitsa, kenako inu munadzampanga iye woyeramtima. Iye anakudutsa inu pomwe apo, ndipo inu simunamudziwe iye.

Eliya anawadutsa, iwo sanamudziwe iye. “Chidempete chakale!”

<sup>74</sup> Khristu anawadutsa, iwo sanamudziwe Iye pambuyo pa imfa Yake, kuikidwa mmanda, ndi chiukitsiro. Mulungu amakhazikitsa izo. Ndipo izo mwamtheradi zimakoka ubweya pa maso a wosakhulupirira. Ndipo zinawonetsera . . . Iye anati, “Ine ndinazibisa izo ku maso a anzeru ndi aluntha, ndipo ndinaziululira izo kwa makanda amene angaphunzire.” Khristu anamuthokoza Mulungu chifukwa chochita izo. Mukuona?

Dzichepetseni nokha. Khulupirani izo. Ayeseni Mawu.

<sup>75</sup> Yesu anati, “Fufuzani Malemba, pakuti mwa iwo inu mukuganiza kuti muli nawo Moyo Wamuyaya, ndipo iwo ndi iwo amene akuchitira umboni za Ine. Inu mumayenera kulidziwa oralo.” Anati, anawauza Afarisi, “Onyenga inu, mumakhoza kuzindikira nkhope ya mumlengalenga; Koma zizindikiro za nthawi, simungathe kuzizindikira. Pakuti ngati inu mukanandidziwa Ine, inu mukanalidziwa tsiku Langa.” Linawadutsa iwo, sanalidziwe ilo mpaka izo zitachitika. Zindikirani tsopano Mawu akukhala ofunikira kwambiri!

<sup>76</sup> Ndipo zindikirani china, pamene ife tiri pa zimenezo, Loti. Yesu anati, Iyemwini, “Kumbukirani mkazi wa Loti.” Ngati Mawu sali ofunikira kwambiri, ngati kulingalira kuli kwabwino; pamene Mngeloyo ameneyo ananena kwa Loti ndi banja lake, “Pitani ku Zoari, koma musakayang’ane mmbuyo!” Ndipo mkazi wa Loti, pa chinthu chaching’ono chopanda ntchito ngati kutembenuka ndi kuyang’ana mmbuyo, koma izo zinali zosiyana ndi Mawu, iye anasanduka chulu cha mchere.

<sup>77</sup> Kenako inu mukuti, “Kuwausa akazi za kumeta tsitsi lawo, kuvala zovala . . .?” Mulungu anati musachite zimenezo! Inu mutsatire Mawu. Loti anali ndi, mosakayika, mkazi wabwino, koma iye sanatsatire Lamulo ku Mawu. Loti! Eva anali mkazi wabwino, koma iye sanatsatire Lamulo ku Mawu; anangolingalira pang’ono ndi izo.

<sup>78</sup> “Kodi sizikumveka mwanzeru, M’bale Branham, kuti ife tizichita izi? Ndine mbadwa ya Amerika, ine—ine ndiri ndi ufulu wochita chirichonse chimene ndikufuna. Umenewo ndi mwayi wanga wa chi Amerika.” Ndi mwayi wanu wa chi Amerika, koma osati mwayi wanu wa Chikristu. Pakuti, mwa Mkristu, ndinu nkhoa; ndipo nkhoa imapinyolitsa maufulu ake. Iyo imakhala chete ndipo imakulolani inu kuchotsa maufulu onse amene ili nawo. Koma mbuzi imakankha namondwe za izo. Uko nkulondola. Koma nkhoa imapinyolitsa maufulu ake. Ndipo Mkristu nthawizonse amapinyolitsa maufulu ake a fuko ngati ali osiyana ndi maufulu anu Achikristu.

<sup>79</sup> Mkazi wa Loti anangoyang’ana mmbuyo, [M’bale Branham akukhwatchitsa chala chake—Mkonzi]. izo zinali zimenezo! Tsopano kodi izo zinachita chiyani? Izo zikutuiza ife apa mwa Abrahamu, ndi Loti, kuti chinthu chimene iwo anachiika apo, chitsanzo. Ndipo ife sitingathe kuchoka kwa izo.

<sup>80</sup> Ahebri, mutu wa 11, anati zinthu izi zinali ngati chitsanzo chathu. Powona kuti tazingidwa ndi mtambo waukulu wotere wa mboni, tikuyenera kusiya pambali tchimo lililonse (Tchimo ndi chiyani? Kusakhulupirira.), tchimo lililonse, kusakhulupirira kulikonse kwa Mawu a Mulungu, kumene kumatifooketsa ife mophweka.

<sup>81</sup> Ife timatsutsana ndi chinachake, nkuti, “Chabwino, iwo amalalikira *icho*, kuti *icho* chinali. . .” Inu musachite zimenezo! Inu muzingochita chimene Mulungu anati muzichita. Muzikhala ndi Iwo, mpaka kumathero!

Mukutti, “Izo sizikupanga kusiyana kulikonse.”

<sup>82</sup> Chabwino, chinthu chokhacho chimene ine ndinganene ndi chimene Mawu amanena. Ndipo Yesu ananena motsimikiza kuti, “Kumbukirani mkazi wa Loti.” Iye anangoyang’ana pa phewa lake. Eva anangoyima kwa kanthawi. Ndizo zonse zimene iye anachita. Mkazi wa Loti anangoyang’ana mmbuyo. Ndipo ngati. . . Mulungu anamusandutsa munthu wolungama uja, Loti, mkazi wake, kukhala chulu cha mchere, chifukwa cha kanthu kakang’ono kwambiri, basi pakusamvera Malamulo Ake mokwanira kungoyang’ana mmbuyo ndi kuwona chimene moto wonsewo unali, ndipo iye anasanduka chulu cha mchere, ndipo akuyima pamenepo lero ngati chitsanzo kuti Mulungu amatanthauza chimene Iye wanena.

<sup>83</sup> Oh, ngati chikhulupiriro chenicheni chingazikike mwa anthu! “Chikhulupiriro chimadza pakumva, kumva Mawu a Mulungu.”

<sup>84</sup> Eva anayima kwa kanthawi. Ndizo zonse zimene iye ankayenera kuchita. Satana anamugwira iye, ndipo anangolingalira izo ndi iye. “Kodi sizikumveka zanzeru? Ngati Mlongo *Wakuti-ndi-wakuti* angachite zimenezo, kodi inu simungachite izo, inunso? Iye ndi mkazi wa m’busa.” Ine sindikusamala yemwe mkaziyo ali, kapena yemwe mwamunayo ali. Ngati izo ziri zotsutsana ndi Mawu, inu musamvetsere izo. Muzingopita molunjika! Zitsanzo!

<sup>85</sup> Umo ndi mmene Abrahamu anachitira. Mukuganiza kuti ndi kulingalira kotani kumene a—sayansi ya zamankhwala ikanamupatsa iye, ya tsiku limenero, kuti iye sakhala ndi mwana ameneyo? Nanga bwanji pamene iye anali wa sevente-faivi? Ndiye ife tikumupeza iye pamene iye anali handiredede, iye ankakhulupirirabe izo mwamphamvu kuposa momwe iye ankachitira poyamba, anali ndi zaka twente-faivi kuti apitirize kumanga chikhulupiriro chowonjezereka pa icho. Ndikuzikonda zimenezo. Inde, bwana.

<sup>86</sup> Ndiye ndikufuna kuti ndibweretse chidwi chanu ku chinthu china tisananyamuke. Kodi inu munazindikira? Ine—ndikuyembekeza kuti mwamvetsa izo. Pa pangano limenero likutsimikiziridwa, polemba pangano limenero ndi kuling’amba

ilo pakati, kodi inu munamvetsa zimenezo? Kwezani manja anu ngati inu munatero, inu munamvetsa chimene izo zimatanthauza. Pangano linkalembedwa, limang'ambidwa, Mulungu akutenga mawonetseredwe a utatu, kuwapanga iwo kukhala mmodzi; kuling'amba ilo pakati, kulitengera thupi Mmwamba, ndi kutumizanso Mzimu Woyera kuti udzakhale mu Mpingo, kuti udzapange chinthu chomwecho chimene thupi limenero linabala, monga mkazi, Mkwatibwi; Mzimu womwewo, ntchito yomweyo, Chiphunzitso chomwecho, chirichonse ndendende basi momwe Iye anakhalira nacho icho, chizindikiro chomwecho, "Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse." Zindikirani!

Pakhoza kukhala, mwinamwake, Myuda wakhala apa.

<sup>87</sup> Mwaona, Mulungu amachita zinthu zimenezo, ndipo izo zimapitirirabe pakati pa anthu ndipo komabe iwo samazimvetsa izo.

<sup>88</sup> Monga momwe ndimafotokozera chifukwa chimene akazi amaphimba nkhope zawo akamakwatiwa. Chifukwa chiyani? Iwo mwina sangamvetse zimenezo. Koma chimene iwo akuchita, nchakuti, podziwa kuti iwo ndi thupi, alibe mutu, mwamuna ndiye mutu wawo. Ndi chifukwa chake Rebekah anadziphimba yekha. Ndipo ndi chifukwa chake Mpingo ukuyenera kudziphimba wokha ndi kudzipereka wokha kwa Khristu, chifukwa Iye ndi Mutu, ndipo Iye ndi Mawu.

<sup>89</sup> Tsopano, Myuda, Yom Kippur, pamene iwo akutenga mgonero, kapena Pasaka, aliyense amadziwa, ameneyo ndi Myuda, ndipo amadziwa kuti pansi pa chivinikirocho pali chidutswa chonyemedwa cha mkate. Ndipo palibe Myuda amene ine ndikumudziwa, amene ine ndinayamba ndayankhulapo naye, amene angathe kufotokoza chifukwa chiyani chidutswa chonyemedwa cha mkate chimenecho. Bwanji, apa izo ziri mu kutsimikizira kwa pangano, thupi lonyemedwa la Khristu, pamene Iye anamunyema Mulungu kuchokera kwa munthu; Iye anali ziwiri zonse Mulungu ndi munthu. Ndipo pamene Iye anawutengera Mzimu mmwamba...Ndipo Yesu anati, mvetserani, "Pa tsiku limenelo mudzazindikira kuti Ine ndiri mwa Atate, Atate mwa Ine; Ine mwa inu, ndi inu mwa Ine." Ndi Mulungu mwa anthu Ake! Mulungu yemweyo!

<sup>90</sup> Iye anaimirira pamenepo, pamene ife tinayankhula usiku wathawu. Mulungu anabwera pansi pano, chilembo chachikulu A-m-b-u-y-e, Yehova-Yire, Yehova-rafa, Yehova-manasse, Elohim, Mmodzi wokwanira mu Zonseyo, Wamphamvuyo, Wamabere-Uyo, maudindo Ake onse ndi chirichonse, zinawonetseredwa mu thupi la munthu amene amadya chakudya cha munthu, ndipo anadzasowa pamaso pawo. Mulungu!

<sup>91</sup> Ndipo Yesu, pamene Iye anabwera, Iye anati, "Monga zinakhalira mu tsiku limenero, chomwechonso izo zidzakhala."



Mulungu!

<sup>92</sup> Ndiwo mkate wonyemedwa pansu pa chivinikirocho, chidutswa chonyemedwa; osati chimene iwo amadya, koma Chimene chimanyemedwa. Nchifukwa chiyani iwo samazimvetsa zimenezo?

<sup>93</sup> Mwa njira yomweyo pamene Yesu ananyamula a—pepala la zikopa ndikuyamba kuwerenga. Iye anawerenga gawo la ndimeyo, ndipo analisiya ilo, lina lonse la ilo, chifukwa ilo linali la Iye basi la tsiku limenero. Ndime ina yonseyo inali yokhudza Kudza Kwake Kwachiwiri.

<sup>94</sup> Ndi chifukwa chake Ayuda samamvetsa zimenezo, chifukwa iwo ankayenera kuti achititsidwe khungu. Iwo sanamuwone Mesiya wawo, ndipo komabe Iye anali kumeneko. Ndipo nthawi iliyonse akamatenga wawo—Paska wawo, pamakhalanso mkate wonyemedwa, ndipo osadziwa izo.

Ine ndinamufunsa rabbi. Iye anati, “Ife timaphunzitsidwa kuti tizichita zimenezo.”

Ine ndinati, “Nchifukwa chiyani inu mumachita zimenezo?”

Iye anati, “Ine sindikudziwa. Palibe aliyense amadziwa.”

<sup>95</sup> Mwaona, mkazi amaphimba nkhope yake, komabe iye samazindikira. Mmalo mobwera ndi kudzamalola mwamuna wake kukhala mutu wake, iye akudzakhala mutu wa mwamuna. Uko nkupotoza. Tsopano ndiko kachitidwe ka Achimerika.

<sup>96</sup> Koma ndi zimenezo, mkate wonyemedwa. Ndiye kenanso ife tikuzindikira, kachiwiri ine ndimafuna kuti ndizindikire apa, mu maziko tsopano ife tisanafike ku gawo lenileni limene ife tikufuna kuti tiyankhulepo usikuuno.

<sup>97</sup> Usiku wathawu inu mukukumbukira kuti pamene Abrahamu, pangano linapangidwa ndi Abrahamu ndi Mbewu yake pambuyo pake. Tsopano, panali Mbewu yachibadwa ya Abrahamu, mwa kuchita kwa chikhulupiriro inabala izo; koma Mbewu yeniyeni ya Abrahamu inali Khristu, Baibulo . . . imene inali Mbewu yachifumu ya Abrahamu. Tsopano zindikirani.

<sup>98</sup> Abrahamu, chiwonongeko cha moto chisanachitike mu tsiku lake, panali chizindikiro chinachitidwa kwa Abrahamu, gulu Lake losankhidwa. Ndipo izo zinali, Mulungu anatsika mmawonekedwe a munthu, anatembenezira nsana Wake ku hema kuchoka kumene kunali Sarah, ndipo ananena zimene Sarah ankanena mu hema. Ndipo Yesu anabwera pamenepo ndipo anati chinthu chomwecho chikanadzakhala pa mapeto a m’badwo. Tsopano, ameneyo anali Abrahamu.

<sup>99</sup> Kenako mbewu yake yachibadwa, pamene Mesiya adzaza. Ndipo Simoni anabwera kwa Yesu, ndipo Iye anamuuzza iye kuti dzina lake linali Simoni, ndipo iye anali mwana wa Yonasi, akudziwa chinsinsi cha mtima wake. Anamuuzza Filipino . . . kapena Natanieli, amene Filipino anamupeza, “Ndinakuwona

iwe pamene unali pansi pa mtengo.” Anamuuzwa mkazi wa pa chitsime, “Iwe unali ndi amuna faivi”; ndipo iye anati, “Bwana, ine ndazindikira kuti Ndinu mneneri.” Mwaona, mapeto a mbewu ya chibadwa ya Abrahamu inalandira chizindikiro chimenecho.

<sup>100</sup> Ndipo izo zinanenedweratu ndi Mbewu yachifumu Iyemwini, Khristu, kuti Mbewu yachifumu, pa mapeto a masiku ake, ikanadzapeza chinthu chomwecho. Tsopano ine ndikuyembekeza kuti tikuzimvetsa zimenezo.

<sup>101</sup> Anamusintha iye. Zindikirani, Mulungu anasintha dzina la Abrahamu. Ine kulibwino ndizisiye zimenezo. Ine ndikadzabwerera ku chitsitsimutso chachitali, ife tidzapita mu zimenezo. Iye ankayenera kuti asinthe dzina kuchoka pa dzina la padziko lapansi, kupita ku dzina loperekedwa ndi Mulungu.

<sup>102</sup> Inu mukuti, “Kodi dzina la munthu lingachite chiyani ndi chirichonse?” Oh, m’bale, ngati inu mukanangodziwa! Bwanji, ena a maina amakono awa amene ife tiri nawo! Ine sindikufuna kuwatchula iwo, chifukwa izo zipweteka kumverera kwanu. Koma Mulungu ali ndi maina amene amatanthauza zinthu, amasintha njira yonse. Oh, inu mukuti, “Zamkutu!”

<sup>103</sup> Nanga bwanji—nanga bwanji Yakobo? Iye asanakhale kalonga pamaso pa Mulungu, ankayenera kusintha dzina lake kuchoka pa Yakobo kukhala Israeli. Nkulondola uko? Ndithudi. Paulo; Saulo ankayenera kusintha dzina lake kukhala Paulo. Oh, ndi angati amene ife tikangawatchule, ndi kunena kuti Mulungu anasintha dzina lawo! Abram ku kukhala Abrahamu, Sarai kukhala Sarah, kusintha dzina lawo. Oh, mai! Ndi dalitso bwanji, kulowa mu mpingo winawake waung’ono ndi gulu losankhidwa, ndi kupita kukaphunzitsa zimenezo, kuwona ma aleluya mu mtima, pamene inu muwona chimene Mulungu amachita.

<sup>104</sup> Tsopano, usiku wathawu ine ndimafotokoza za “pakati pa mzere” ndi “kutsimikizira izo.” Ndikufuna ndingogunda izo ndisanalowe mu nkhani yanga. Kutu, Mulungu anamusintha Abrahamu kuchoka kwa mwamuna wokalamba wamakwinya, iye ndi Sarah, kubwerera kudzakhala banja laling’ono, anasintha umunthu wawo asanalandire mwana wolonjezedwayo. Chizindikiro chotsiriza chimene iwo anali nacho chinali mawonetseredwe a Mulungu mu thupi, amakhoza kuwerenga mtima wa mkazi kumbuyo kwa Iye, mu hema. Ndipo chinthu chotsatira chinali chakuti matupi awo anasinthidwa. Tsopano, usiku watha ine ndimachedwa, ndipo ine ndimatha kumverera ena akudabwa nazo izo. Ndikufuna ndizibweretsebe izo pafupi pang’ono.

<sup>105</sup> Tsopano, umboni wake unali wakuti, pamene iwo onse awiri anayenda ulendo wautali umenewo, iwo mwamtheradi anali atasinthidwa. Ndipo Baibulo linati, “Awiri onsewo anali

okalamba kwambiri. Ndipo thupi la Abrahamu linali ngati lakufa, ndipo chiberekero cha Sarah chinali chakufa.” Kodi izo zinali zolondola? Tikudziwa kuti iwo anali akufa, koma Mulungu anawasintha iwo. Tsopano kuti atsimikizire izo kwa inu, kuti Iye anachita zimenezo. Choyamba, chifukwa chiyani Mfilisti uja (kapena osati. . .), inde, ndikukhulupirira kuti inali mfumu ya Afilisti, inagwa mchikondi ndi Sarah, mkazi wokalamba? Ndipo iye anali wokongola pomuyang’ana.

<sup>106</sup> Chinthu china. Pamene Isaki anabadwa, ndipo Sarah ndi Abrahamu anali okalamba, akukonzekera kuti afa, kenako iwo anakhalabe moyo, ndipo Isaki anakwatira pamene iye anali wa usinkhu wa zaka forte; Sarah anafa. Ndipo Abrahamu anakwatira mkazi, Ketura, ndipo anali ndi ana aamuna faivi, sikisi, ine ndikukhulupirira iwo anali, pambali pa ana aakazi, zitachitika zimenezo; ndipo apa, zaka sikisite zapitazo, iye anali ngati wakufa! K-e-t-u-r-a-h, Keturah. Iye anakwatira Keturah, zaka fifite kapena sikisite zitachitika zimenezo, ndipo anabereka ana aamuna sikisi pambali pa ana ake aakazi; ndipo zaka sikisite mmbuyo mwake, iye anali ngati wakufa. Aleluya! Ndi zimenezotu! Lonjezo la Mulungu ndi lotsimikizika. Ameni. Oh, ine ndikuzikonda Zimenezo!

<sup>107</sup> Kuti mungofika kwa inueni ndi kuwerenga! Lero, mmbuyo mu nkhalango, ndikuwerenga, ine ndiri ndi chinachake chaching’ono chimene ine ndikufuna kuti ndichifotokeze.

<sup>108</sup> Israeli. Anthu a Mulungu tsiku lina anali ku Igupto, anagulitsidwa mu ukapolo, ndipo sakanatha kudziletsa kukhala kumeneko. Dongosolo lalikulu lokonzedweratu la Mulungu linawatumiza iwo kumeneko. Iye anali atamuza Abrahamu kuti adzakhala mlendo m’dziko lachilendo kwa zaka foro handirede. Ndipo kumeneko iwo anadzakhala ngati anthu ena onse, ndipo iwo anali akapolo. Ngati a—ngati mwamuna wa ku Igupto akafuna kuwachita zoyipa atsikana Achihebri, palibe chimene chimanenedwa. Ngati iwo akafuna kupha anyamata awo, iwo ankawapha iwo, palibe chimene chikananenedwa. Iwo anali akapolo. Iwo ankawatayira iwo mkate wawo wowumbidwa. Ankadya iwo, kapena kukhala osadya; akadandaula, amaphedwa! Anali malo otani kwa anthu a Mulungu!

<sup>109</sup> Koma tsiku lina, aleluya, Mulungu anakumbukira lonjezo Lake kwa Abrahamu. Ulemelero! Tsopano ine ndikuyambanso kumverera mwachipembedzo. Zindikirani, Mulungu anakumbukira lonjezo Lake kwa Abrahamu. Ndipo Iye anamudzoza mneneri, ndi Lawi la Moto pa iye, ndipo anabwera uko mdzikolo ndipo anayamba kuwakumbutsa iwo za lonjezo la Mulungu limene silikanakhoza kulephera. Ndipo Mulungu analipo kuti atsimikizire Mawu Ake. Kulondola. Iye anawauza iwo za dziko limene linkayenda mkaka ndi uchi, Mulungu anali atalipereka ilo kwa iwo. Iwo anaguba kutuluka

mu Igupto pa mphamvu ya umboni wa mneneri uyu ndi Lawi la Moto pa iye, chifukwa iye anatumidwa. Ndipo Mulungu anali atatsimikizira kuti Iye anali ndi iye.

<sup>110</sup> Tsopano pamene iwo anafika pa malo otchedwa Kadeshi-barnea. Iwo anali nthawi ina mpando wachiweruzo wa dziko lapansi, Kadeshi-barnea. Ndipo kumeneko iwo anali ndi wankhondo pakati pawo, dzina lake Yoswa. Ndipo mawu akuti *Yoswa*, mu Chihebri, amathanthauza “Yehova-mpulumutsi.” Ndipo Yoswa, wankhondo wamkulu. . . Tsopano kumbukirani, iwo anali asanaliwonapo dziko ili, iwo anali atangomva za ilo. Inu mukuona choimiracho tsopano? Iwo anangomva za dzikolo. Iwo anali atasiya zonse kuti apite ku dziko ili, chifukwa Mawu a Ambuye anali atabweretsedwa kwa iwo, ndipo anatsimikizira kuti iwo anali panjira yawo yopita kudziko ili. Ndi choyimira chotani cha Mpingo, panjira yawo, osadziwa kalikonse za ilo, palibe mmodzi wa iwo amene anayamba wakhalapo kumeneko. Koma Yoswa, pamene iwo anayandikira malire, pa Kadeshi, mpando wa chiweruzo, kumene chiweruzo chinakantha Israeli, kuchokera kwa mmodzi amene anali atapitako ndi kubwerera. Ndipo Yoswa anawoloka Yordano, kupita ku dziko lolonjezedwa, ndipo anabweretsanso umboni kuti izo zinali ndendende basi zimene Mulungu ananena kuti izo zinali. Ndipo anatha kulawa mphesa zimene zinabzalidwa mdziko losangalatsalo.

<sup>111</sup> Tsopano, iwo anali atalonjezedwa kuti iwo akhoza kukakhala ndi nyumba kumene iwo angakhoze kukakhala afulu, iwo akhoza kukalera ana awo mwaulemu ndi—ndi mwamantha aumulungu, kukakhala ndi mpingo, ndi zina zotero. Iwo anali okondwa bwanji kuwoloka dzikolo ndi kukatenga nyumba iyi, kuchoka pokhala akapolo. Zindikirani. Koma pamene iwo anawoloka, anakhala miyoyo yawo, icho chinali chinthu chachikulu. Koma potsiriza mapiriwo anaphimbidwa ndi mitumbira. Iwo anakalamba ndipo anafa, anakalamba ndipo anafa, anthu a Mulungu.

<sup>112</sup> Kenako tsiku lina kunadza Wankhondo wina wamkulu, wamkulu wa onsewo, Yehova-Mpulumutsi, *Yesu*, Iye anabwera, ndipo Iye anati, “Ulipo Moyo kuseri kwa imfa! Pakuti, mnyumba ya Atate Anga muli nyumba zambiri. Ngati kukanakhala kuti sichoncho, Ine ndikanakuuzani inu. Ine ndipita ndi kukakukonzerani malo, ndipo ndidzabwereranso kudzakulandirani inu kwa Inemwini.” Ndipo Wankhondo wamkulu uyu anadza ku Kadeshi-barnea Wake, mpando wachiweruzo wa ife tonse, Kalvare! Pamenepo Iye anatenga pa Iye kusaweruzika kwa ife tonse. Ndipo Iye anawoloka mtsinje wa Yordano umene ife timawutcha imfa. Ndipo pa tsiku lachitatu Iye anauka kachiwiri, monga Yoswa akubwerera kuwoloka mtsinje, akubweretsa umboni kuti “munthu amene anafa akhoza kukhalanso ndi moyo.”

<sup>113</sup> Ndipo Iye anati, kuti mupange kwanu. . . kutsimikiza za

inu, “Ine ndikufuna inu mupite kumeneko ku mzinda wa Yerusalemu, ndi kukadikirira kumeneko. Ine ndikupatsani inu chikole cha Izo. Ine ndidzakupatsani inu umboni, chikole.” Ndipo iwo anapita ku mzinda wa Yerusalemu ndipo anakadikirira mpaka Moyo Wamuyaya unabwera ngati mphepo yamkokomo yamphamvu.

114 Ndipo lero, zitatha zaka thuu sauzande, ife tikadali nawobe umboni umenewo kuti ife tadutsa kuchokera ku imfa tapita ku Moyo. Yoswa wathu wabweretsanso umboni, ndipo ife tiri panjira yathu yopita ku Dziko lolonjezedwa, kulawa za mphatso zakumwamba za Mulungu zimene Iye wazibweretsa kwa ife. Zindikirani izo, nzodabwitsa bwanji! Yang’anani kumene inu munali poyamba. Chidakhwa . . .

115 Ine ndinakumana ndi m’bale lero; anali ndi kumverera kwachilendo kuti akhote msewu winawake, ndi kuchokapo. Ine ndaiwala kuti dzina la munthuyo linali chiyani. Iye akhoza kukhala pano mu msonkhano. Komabe, ngati iye mulibemo, bwanji, Mulungu anali wabwino kwa iye. Iye ndi wa Chimwenye, Mmwenye watheka. Iye ndi wochokera ku Virginia. Mzimu Woyera unanena kwa ine, osati kumanena izo. Ndinali nditamutulutsa mkazi wanga. Anati, “Pita kumusi njira *iyi*, ndipo ukakhote ngodya *iyi*.” Ine ndinapita kumusi uko. Oh, izo zimachitika nthawi zonse. “Ukadikirire pomwe *apa*.” Kenako ndinakadikirira pamenepo kwa maminiti angapo. Anati, “Tembenuka ndipo ubwerere kumtunda njira *iyi*.” Ndipo, pamene ine ndinatero, ine ndinakakumana naye iye.

116 Iye anati, “M’bale Branham, ine ndikukudziwani inu.” Anati, “Ine ndinabwera ku Jeffersonville nthawi ina, ndi kudzakupezani inu.” Ndipo anati ine . . . “Inu munali kutsidya kwa nyanja.” Koma iye anakhala woledzera, mmoyo wake. Ine ndinagwira dzanja lake, iye osadziwa chimene ndinali kuchita. Ndipo anali ndi matenda a chiwindi. Pamene ine ndinali nditaimirira pamenepo nditagwira dzanja lake, kunjenjemera kunandichokera ine. Chiyani? Iye anachiritsidwa. Pomwepo pa ngodya ya msewu, iwo anamva izo mu mzinda wanu.

117 Ine sindikudziwa yemwe mwamunayo . . . Kodi iye ali pano? Ine sindikudziwa. Ngati iye alipo, iye . . . Ine—sindikudziwa. Iye anati iye—iye ankafuna kubwerera kwawo. Ine ndikuganiza kuti iye ankayenera kupita. Iye anali—mwamuna Wachimwenye, ine ndikuganiza iye anakwatira a—mkazi wachizungu. Ndipo anali wochokera ku Virginia. Ndipo ndaiwala dzina lake. Iye ankakhala kumusi kuno kuzungulira Logar kapena chinachake chonga chimenecho. Ndipo iye anali njira yonse ya ku Jeffersonville. Koma iye anali ndi kumverera kuti ayende kupita pa ngodya; Mzimu Woyera anati, “Pita kumusi njira *iyi*.” O Mulungu, ndichitireni chifundo! Ndi zimenezotu.

118 Ine ndikhoza kutenga maora pambuyo pa maora, kukuuzani

inu zinthu zimene ine ndazona zikuchitika ndi kuchitidwa monga choncho. Chifukwa chiyani? Yesu, Wankhondo wathu wamkulu, anapita uko ndipo anakagonjetsa dzikolo, anakagonjetsa imfa, anakagonjetsa gehena, anakagonjetsa manda, anauka tsiku lachitatu, ndipo anati, “Ine ndine Iye amene ndinali wakufa, ndipo ndiri wamoyo kwanthawizonse, ndipo ndiri ndi mafungulo a imfa ndi hade.” Ndi ameneyo Mgonjetsi, popeza Iye anang’amba chophimba pakati. Ndi Uyo wayimayo!

<sup>119</sup> Monga mlongo wachikuda wachikulire. Mundikhululukire ine, abwenzi anga achikuda muno. Iye anali kuchitira umboni pamsonkhano, ndipo iye anali wakummwera kwenikweni mu kuyankhula kwake. Iye anati, “Chabwino, ine ndikufuna kuti ndikuuzeni inu nonse chinachake usikuuno.” Iye anati, “Ine ndithudi sindiri chimene ine ndikuyenera kukhala.” Ndipo iye anati, “Ine ndithudi sindiri chimene ine ndikufuna kuti ndidzakhale. Koma chinthu chimodzi chimene ine ndikuchidziwa, ine sindiri chimene ine ndinali.” Chotero iye anali atabwera kwinakwake!

<sup>120</sup> Ndipo ine ndikuti, ndi zimenezo usikuuno! Nthawi ina tinatayika mu tchimo. Ndipo lero, povomereza umboni, lonjezo lobwezedwa (chikole pa chipulumutso chathu Chamuyaya), ife tawuka kuchokera ku imfa tapita ku Moyo, ndipo tikukhala pamwamba pa ilo. Kodi chidzakhala chiyani pamene tidzalandira malipiro athunthu, ndi kudzawoloka mtsinjewo, ifeeni, kudzalowa mu Dziko laulemerero ilo?

<sup>121</sup> Mayeso aakulu! Tsopano Abrahamu, pambuyo pa zinthu zodabwitsa zonsezi, iye anayesedwa atalandira mdalitso. Abrahamu anayesedwa.

<sup>122</sup> Tsopano pamene ndi pamene anthu amalephera. Tsopano, mvetserani mwatcheru kwenikweni tsopano, musaphonye izi. Baibulo linanena, kuti “Mwana aliyense amene amabwera kwa Mulungu amayenera kudzudzulidwa, kulangidwa, kukwapulidwa. Ndipo ngati ife sitingathe kupirira kulangidwa, ife timakhala ana apathengo, ndipo osati ana a Mulungu.” Izo zimatsimikizira kuti chikhulupiriro chathu sichinali chimene ife tinati chinali, tiribe chimene timadzinenera kuti tiri nacho. Tsopano ife tikufika mu Chikalvini china chabwino kwenikweni tsopano, chotero ife tikuyenera kusamala zimenezo. Tsopano zindikirani, “Mwana aliyense amene abwera kwa Mulungu akuyenera kudzudzulidwa, kulangidwa,” Mawuwo amamukwapula iye ndi kumudula iye mzdutswa, kugwetsera pansi kachikhulupiriro kalikonse ka pansi pa iye; mwaona, kuyesedwa, ndi kuwona ngati iye ali mwana wa Mulungu.

<sup>123</sup> Tsopano Abrahamu, atatha kulandira mdalitso, kenako pambuyo pake anayesedwa.

124 Kodi nthawi imeneyo imapita kuti? Sindinamalize nkomwe mutu wanga, ndipo ndi nthawi yoti nditseke. Kodi mungapirire nane maminiti ena fifitini? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Zikomo inu. Khalani olemekeza. (Abrahamu. Yang’anani pa Nowa.) Tiyeni titenge izo kwa mphindi chabe. Ife sitingathe kuthamange; palibe kusowejera. Ndipo, mai, kodi ife tikuthamangira chiyani? Ine ndangokhala wochedwetsa. Ine—ine sindiri monga anyamata ena awa amene amatha kuyima, ndikungopemerera izo monga choncho. Ine—ine—ine ndi wochedwa, ndimayenera kudikirira mpaka Iye atapereke izo kwa ine.

125 Tayang’anani pa Nowa, Mulungu atamupangitsa iye kulalikirira zaka handiredede ndi twente, mkati momwe mwa dziko lalikulu la sayansi kuposa limene ife tiri nalo lero. Oh, ndithudi, iwo ankamanga mapiramidi. Ife sitingathe kumanga iwo. Iwo ankamanga sphinx. Sitingakhoze kumanga iyo. Iwo ankaumitsa mitembo kuyipangitsa iyo kuti iziwoneka mwachibadwa mpaka lero. Ife sitingakhoze kuchita zimenezo. Iwo anali ndi utoto umene ankatha kuyika mu zinthu, kuti mtunduwo ukhale kwa zaka foro sauzande usanasinthe. Ife tiribe zimenezo. [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi]. Ndipo izo zinawonetsera kuti iwo anali ndi chitukuko monga chimene Yesu anati, “Monga zinali mmasiku a Nowa.” Ndipo Nowa, mu dziko lasayansi limenelo, akulalikirira, “Mvula idzagwa kuchokera kumwamba, chifukwa Mawu a Mulungu ananena chomwecho!” Nowa anali mneneri.

126 Ndipo pamene inu muwawona aneneri akuwuka, inu kulibwino muwonetsetse, chiweruzo chiri pa njira yake.

127 Chotero ndiye Nowa akulalikirira, ndipo anthu akuzikana izo, ankamuseka pa nkhope yake. Ine ndikukhoza kulingalira ena a iwo anati, “Izo sizikugwirizana ndi kuvomereza kwathu kwasayansi.” Huh!

128 Ine ndikulingalira, chinthu chomwecho monga izo ziri lero. Iwo amanena kuti, “Kufuula ndi kutamanda Mulungu, ndi kulira, ndi izi apa zotchedwa moyo wa ‘woyera-wodzigudubuza’ ndi zinthu, zonsezo ndi kutengeka kwa maganizo.” Izo sizikugwirizana ndi kuvomereza kwawo kwa sayansi, koma zikugwirizana ndi Baibulo la Mulungu. Ndicho chinthu chachikulu. Zindikirani.

129 Ndikuganiza sayansi inatuluka ndipo inati, “Taona, mzanga. Taona, ndiwe—iwe ukukhala ngati wazungulira mutu. Tayang’ana apa. Ine, ife tiri ndi chombo, tikhoza kuwombera mwezi kapena kutumiza Sputnik kumeneko. Kulibeko dontho limodzi la madzi pakati pa kuno ndi kumeneko. Tsopano iyo ikuchokera kuti?”

130 Ine ndikukhoza kumumva Nowa akuti, “Mulungu ananena chomwecho! Ndipo ngati Mulungu anati izo zinali chomwecho,

Iye ndi Yehova-Yire, Iye akhoza kupereka madzi kumeneko. Mulungu wanena chomwecho! Izo zichitika, mulimonse!” Wina anati. . .

<sup>131</sup> Inu mumutenge munthu akufa ndi khansa, mthunzi wa munthu, ndi uyu apa; chaka chamawa iye ndi munthu wabwino wathanzi. Izo zinachitika motani? Anamugoneka iye kumbuyo. . . Ndiri nawo mahandirede a maumboni amenewo. Munthu anali atachoka mmoyo uno, dokotala anasaina chi pepala, “Iye wamwalira, wamwalira kwa maora ndi maora.” Ndipo Mulungu anapereka masomphenya, ndipo iye ali moyo tspano. Motani? Musandifunse ine. Ine sindikudziwa. Koma Mulungu anati, “Chiritsani odwala, ukitsani akufa, tulutsani ziwanda.” Uko nkulondola.

<sup>132</sup> Pamene inu mukudwala ndipo Mulungu nkulengeza machiritso, inu muzingopitirira—kumapitirira ndi dokotala wanuyo, kumusiya iye akuuzeni inu mukakhala bwino. Iye adzakupatsani inu. . . Izo zidzapereka umboni kwa iye. Pamene iye akuti, “Chabwino, zonse zapita”; ndikuti, “Mulungu alemekezeke! Zikomo, dokotala, chifukwa cha ntchito yanu,” ndipo kapitirirani. Mukuona? Uko nkulondola. Zindikirani.

<sup>133</sup> Tsopano Nowa, iye anati, “Kukubwera mvula, dziko lonse lapansi, idzakusesani anthu oyipa inu.”

<sup>134</sup> “Ah, zamkutu! Ife tiri ndi mipingo yathu. Abusa athu samanena zinthu zonga zimenezo. Munthu wokalambayo wapenga, akumanga chombo kumtunda uko. Inu mukuganiza kuti ali yense akhulupirira zimenezo?”

<sup>135</sup> Tsiku lina, Mulungu anati, “Ndamva kunyoza kwawo mokwanira. Ndakonzeka tsopano. Lowa mkati!” Ndipo apa pakubwera zinyama, ziwiri ziwiri, chingolopiyo wammuna ndi wamkazi, mpheta yaimuna ndi yaikazi, mbuzi yaimuna ndi yaikazi, nk'hosa yaimuna ndi yaikazi, mkango, nyalugwe, zonse zimene zikupuma mpweya pa dziko lapansi, zinalowa mu chombo.

Nowa anati, “Ndicho chizindikiro chanu chomaliza!”

<sup>136</sup> Ndipo sanakhulupirire izo. “Pita mmwamba ndipo ukakhale ndi nyama zako zonunkhazo.”

<sup>137</sup> Apo iye anali, Nowa akumumvera Mulungu. Zinalibe kanthu chimene dziko linkanena, iye anamvetsera kwa Mulungu; iye anali mneneri. Iye analowa mchombo, ndipo Mulungu anatseka chitseko kumbuyo kwake.

<sup>138</sup> Tsopano ine ndikhoza kulingalira, ena mwa okhulupirira ammalire, amene anakhala mozungulira ndi kumamvetsera uthenga wa Nowa, ndipo anakhala patali, inu mukudziwa, iwo anati, “Inu mukudziwa chiyani, nkhalamba imeneyo mwina imalondola. Tiyeni tipite kumeneko ndipo tikayime pafupi. Iye anati, ‘Iyamba kugwa mvula pamene chitseko



chiti chitsekedwe.’ Mulungu anamuuya iye kuti Iye adzatseka chitsekocho, iyo idzayamba kuvumba. Tiyeni tipite ndipo tikaime pafupi. Ndipo ngati ingayambe kuvumba, ife tikagogoda pa khomopo. Chifukwa ndi nkhalamba yachifundo, iye adzatsegula chitsekocho.”

<sup>139</sup> Inu mwaona, nthawizina inu mumayang’ana pa wa mthenga mmalo mwa Uthenga. Mulungu anatseka chitseko. Zinalibe kanthu momwe Nowa analiri wantima wachifundo, anali Mulungu amene anachita kutsekako ndi kutsegula, chirichonse chimene Iye akufuna.

<sup>140</sup> “M’bale Branham, pali mwamuna wakhala pansu apa pa kona. Pitani kumusiko ndipo mukamuchize iye, ife tikhulupirira mu machiritso Auzimu.” Ameneyo ndi mdierekezi.

<sup>141</sup> Yemwe uja yemwe anati, pamene anayika chiguduli pankhope Yake, ndipo nkumumenya Iye pamutu, mu pabwalo lamilandu, iye anati, “Ngati Iwe uli mneneri, tiwuze ife amene wakumumenya Iwe tsopano. Ife tikhulupirira izo.” Iye samachitira aliyense zisudzo. “Ngati Iwe uli Mwana wa Mulungu, sandutsa miyala iyi kukhala mkate. Ngati Iwe uli!” Iye akanakhoza kuchita zimenezo, koma Iye samachitira aliyense zisudzo. “Ngati Iwe uli mwana wa Mulungu, tsikatu pa mtandapo.” Azibusa ankanena zimenezo, mwaona. Iye sanamuchitire chisudzo aliyense.

<sup>142</sup> Iye ankangochita monga momwe Atate amuwonetsera Iye, ndipo osati china chirichonse. Ndicho chimene Iye ananena, Yohane Woyera 5:19, “Mwana sangachite kanthu mwa Iyeyekha, kokha chimene Iye awawona Atate akuchichita.” Ndi zimenezotu pamenepo. Zindikirani.

“Ife tipita kumeneko ndipo tikayima mozungulira chombocho, ngati iyamba kuvumba . . .”

<sup>143</sup> Ine ndikulingalira Nowa anati . . . Iye analowa mu chigawo choyamba, anakwera mmwamba mu chigawo chotsatira (mbalame) kuchokera ku zinthu zokwawa, mpaka ku ofesi yotsatira. Kuchokera ku kulungamitsidwa, mpaka ku kuyeretsewa (mbalame), kenako iye anapita kuchokera pamenepo kupita ku ubatizo wa Mzimu Woyera; kumene kunali zenera, kumene kuwala kukanakhoza kulowamo. “Ndakalowa mmwambamwamba, ndakhala pansu.” Anati, “Chabwino, banja, inu amene mwabwera muno ndi ine, mmawa . . . Nthawi ikutha masana ano. Tsopano Mulungu watseka chitseko kumusi uko. Mmawa, kudzakhala mdima padziko lonse. Mmawa, mvula iyamba kuvumba ndipo chombo chidzayandama, ndipo Mulungu adza—adzachepysa aliyense wa ochimwa ankanza amenewo amene sanakhulupirire Uthenga.” Onse a iwo akudikirira.

<sup>144</sup> Mmawa wotsatira, anadzukapo, nayang’ana panja, kokongola ndi kowala. Iye analowa mchombo, ndi angati

akudziwa tsiku limene iye analowamo? Tsiku la chi 17 la Meyi, pamene Nowa anali wausinkhu wa zaka sikisi handirede zakubadwa. Tsiku la chi 17 la Meyi, Baibulo linanena choncho. Ndipo pamene iye analowa mmenemo, tsiku la chi 17 linadutsa, dzuwa linatuluka likutentha basi monga momwe ilo limakhalira nthawizonse.

<sup>145</sup> Ine ndikuwalingalira iwo, ammalire, akuti, “Ah! Ine ndinakuuzani inu kuti kunalibe kanthu kwa izo! Kodi inu nonse mukuzungulira pamenepo chifukwa chiyani? Chokaniko kwa munthu wopanda pake woteroyo!”

“Chabwino, ine ndikuganiza uko kunali kulondola.”

<sup>146</sup> Koma, inu mukuona, pali mzere wolekanitsa umene umapangidwa pakati pa kukhulupirira ndi kusakhulupirira. Ndipo inu mubwera mbali imodzi kapena inayo. Ndipo ilipo nthawi imene umalandira kuyitana kwanu komaliza.

<sup>147</sup> Chotero, tsiku lachiwiri, zinali zokhumudwitsa bwanji kwa Nowa ndi mpingo wake, pamene iye anawauza iwo kuti Mulungu adzawononga dziko lapansi. Koma inu mukudziwa kuti iye anadikirira izo kwa nthawi yayitali bwanji? Masiku seveni, palibe chinachitika. Kuyesa!

<sup>148</sup> Ndipo pa tsiku lachi eyiti, panali mdima padziko lonse lapansi, madontho akulu akulu anayamba kugwa kuchokera kumwamba, madzi anayamba kugwa, ndipo akasupe anaphulika. Misewu inadzaza madzi. Anthu anagogoda pa chitseko, koma Nowa sanawamve iwo nkomwe. Ndipo icho chinayandama pamwamba pa phiri lalitali kwambiri, ndipo onse opanda chombo anawonongeka.

<sup>149</sup> Mulungu akumuyesa Nowa, kuti awone ngati iye akanayesera kukwera pazenera, kapena chinachake. Iye atapanga kale lonjezo, Nowa anadikirira ilo!

<sup>150</sup> Ndi zimenezotu! Pamene iwe uli ndi lonjezo, ndipo iwe ukudziwa kuti ndi lonjezo, ukhale nalo ilo! Abrahamu ankayenera kuti ayese dwe. Kukhala ndi lonjezo!

<sup>151</sup> Tsopano, iwo anapeza chizindikiro chawo chotsiriza. Kenako thupi lawo linasinthidwa. Ndipo mwamsanga Isaki wamng’ono anawonekera powonekera, mnyamata wamng’ono wokondedwa Wachiyuda. Ine ndikulingalira kuti atatha masiku ake eyiti iye anadulidwa. Momwe mayi wamng’ono uyo, usinkhu wa zaka handirede... Momwe Abrahamu, usinkhu wa zaka handirede; kapena nainte zake, ndi iye handirede; momwe iwo akuyenera kuti anali, pafupifupi muma twente awo, akusangalala. Mnyamata wamng’ono uyu, momwe iye analiri wokoma!

<sup>152</sup> Ndipo inu mukudziwa, Mulungu anati, “Tsopano kuwapangitsa anthu mmasiku ali nkudza (Mbewu ya Abrahamu) kudziwa, Mbewu yako ikudziwa kuti Ine ndimasunga lonjezo

Langa kwa munthu aliyense amene adzagwiritsitse ku Mawu Anga, Ine ndimupatsa iye yesero.”

<sup>153</sup> Pamene mnyamata wamng'onoyo anafika pafupifupi usinkhu wa zaka fortini, ine ndikulingalira, tsitsi laling'ono la nyankhalala ndi maso aang'ono okongola (Oh, momwe abambo ndi amayi osangalalawo! Inu mukudziwa momwe inu kholo mumakhalira ndi mwana wanu, mwana yekhayo.), kenako Mulungu anati kwa Abrahamu, tsopano, Iye sakananena izo kwa Sarah, chifukwa Sarah anali chotengera chofooka, ndipo chotero Iye anati, “Abrahamu, ine ndikufuna kuti iwe umtenge mnyamata wamng'ono uyu amene Ine ndakupatsa, iye amene Ine ndidzakupangitse naye iwe kukhala atate wa mafuko ambiri, ndipo Ine ndikufuna kuti umutengere iye pamwamba pa phiri limene Ine nditi ndikuwonetse iwe usikuuno mu masomphenya, ndipo kumeneko ukamuphe iye.” Kuwononga chiyembekezo chokhacho chimene chinalipo kuti iye akhale atate wa mafuko, kuti Mulungu asunge Mawu Ake; Mulungu anati, “Ndikupanga iwe atate wa mafuko.” Iye wadikirira tsopano zaka zonsezi, mpaka iye ali ndi usinkhu wa zaka handirede zakubadwa, usinkhu wa zaka handirede ndi fortini zakubadwa. “Ndipo ndi uyu mnyamata wamng'onoyo tsopano, ndipo umboni wokhawo umene iwe uli nawo kuti Ine ndisunga Mawu Anga, iwe upite uko ndipo ukamuwononge iye. Ine ndikupangabe iwe kukhala atate wa mafuko mwa mwana ameneyu.”

<sup>154</sup> “Ndipo Abrahamu,” anati, “iye sanadzandime pa lonjezo la Mulungu. Iye anadziwa kuti iye anamulandira iye ngati mmodzi wochokera kwa akufa. Anadziwa, ngati Mulungu analonjeza chomwecho, Iye akanadzamuukitsa iye kwa akufa.”

<sup>155</sup> Ndiyeno ndife Mbewu ya Abrahamu? Ndipo cholakwika chimodzi chaching'ono chaumulungu chikhoza kuphulika mu njira, kuti mukhale otchuka ndi amuna ndi akazi ena onse, inu mumapita kwa izo mmalo mokhala ndi Mawu. Manyazi pa inu! Bungwe lina lalikulu, kodi zimenezo zimatanthauza chiyani kwa Mulungu? Iye adzasesa izo munga *choncho!* [M'bale Branham akukhwatitsa chala chake—Mkonzi]. Iye ali kutali ndi izo, wakhala ali chipangireni iwo bungwe, aliyense wa iwo, ndipo nthawizonse adzakhala. Osati munthu payekha mmenemo, koma kachitidwe kabungwe, kamatsutsana ndi Mulungu. Mpingo uliwonse umene wapanga bungwe ndi mayi. . . kapena mwana wamkazi wa bungwe la Chikatolika. Baibulo linanena chomwecho, Chivumbulutso 17, “Hule wakale, ndi ana ake aakazi a hule.” Kulondola ndendende.

<sup>156</sup> Ife tiri naye iye wakhala pomwe pano pa fuko lathu. Manyazi pa inu ma Democrat abwino amene munagulitsa mafulu anu obadwa nawo! Chabwino, ife tizisiya zimenezo zipite, mpaka ine nditadzabwereranso. Zindikirani. Ine ndachedwa. Kodi Khristu wanu samatanthauza zambiri kwa inu kuposa ndale zanu?

Inu mukuyenera kuchita chimene Abraham Lincoln ananena. Chabwino. Zindikirani, tikupitirira patsogolo.

<sup>157</sup> Tsopano Mulungu anati, “Iwe umutenge mnyamata wamng’ono, umutengere iye pamwamba pa phiripo.”

<sup>158</sup> Tsopano inu mukufuna kudziwa ngati Abrahamu anali mnyamata kapena ayi? Iye anayenda ulendo wa masiku atatu ndi mwanayo, ali ndi nkhuni, ndi wantchito, ndi bulu. Tsopano munthu aliyense, munthu wamba. . . Ine ndinkalondera nthambo zamagetsi, ndinkayenda pamene ndinali wolondera zinyama; ndipo ine nditha kuyenda, mophweka, mailosi sarte pa tsiku. Ndipo ife timakhala ndi mapazi a mafuta, ife timazitcha izo. Koma amuna amenewo, mayendedwe awo okha ndi pa mapazi, kapena kukwera bulu. Ndipo apa iwo anali ndi bulu wochedwa pang’ono; ndipo ife tikhoza kumuposa kuyenda kwake. Ndipo apa iye anali, ulendo wa masiku atatu, ndipo kenako anakweza mmwamba mutu wake ndipo analiwona phiri patali, komabe. Iye akuyenera kuti anali pafupifupi mailosi handirede kuchokera ku chitukuko, kutali komwe mchipululu. Tsopano mvetserani, ndipo zindikirani.

<sup>159</sup> Kenako iye anatenga nkhuni ndipo anaziika pa nsana wa Isaki; mtanda, Mwana wa Mulungu patapita zaka. Ndipo Isaki ananyamula nkhuni akukwera phirilo, zimene iye ankati akazigoneke ngati nsembe. Kuwonetseratu!

<sup>160</sup> Ngati Mulungu anawonetseratu izo mpaka pa dontho; Mkazi wa Loti, usatembenuke ndi kuyang’ana mmbuyo ku zinthu za mdziko. Zoyimira zonsezo ndi mithunzi ndi zangwiro. Mukuona? Kumbukirani Eva. Kumbukirani mkazi wa Loti. Kumbukirani Loti iyemwini, mwamuna iwe. Kumbukirani, Adamu anagonjera kwa mkazi wake; Loti, mwanjira yomweyo. Samalani. Ine ndikungokuuzani inu, monga m’bale. Nthawi yatha kuposa momwe mukuganizira.

<sup>161</sup> Zindikirani Isaki wamng’ono akukwera phiri. Ndipo anayamba kukayikira. Ndipo anayang’ana mozungulira, ndipo anati, “Bambo anga?”

Ndipo anati, “Ndine pano, mwana wanga.”

<sup>162</sup> Iye anati, “Apa pali nkhuni. Ndipo apa pali zonse, chirichonse, moto. Koma ali kuti mwanawankhosa wa nsembe yopsyereza?”

<sup>163</sup> Mvetserani kwa abambo okalamba amenewo, opanda kunjenjemera mmawu awo, iye anati, “Mwana wanga, Mulungu adzazipezera Iyemwini nsembeyo.” Mwana wake mmodzi yekhayo akupita kokaphedwa, komabe mtima wakale wokhulupirika uja unadziwa kuti Mulungu sanganame.

<sup>164</sup> Imeneyo ndi Mbewu ya Abrahamu lero! “Izo zingakhale motani, M’bale Branham?” Mulungu adzazipezera Iyemwini!

“Kodi Iye apanga bwanji?” Ine sindikudziwa. Koma Iye ndi Yehova-Yire!

<sup>165</sup> Anakwera pamwamba pa phiri, anagudubuza mwala. Anayika nkhu ni pamiyala, ndi kuziyatsa izo ndi moto. Anati, “Isaki, mwana wanga, tembenuka.” Iye anatenga chingwe mchiuno mwake, ndipo anamanga manja ake ndi mapazi ake. Isaki, womvera, munga Khristu anali, ku imfa. Anamugoneka iye pa thandala. Anafikira mu chikwama chake ndipo anasolola mpeni waukulu; anawunola iwo kangapo, akuyang’ana kumwamba.

<sup>166</sup> “Iye sanadzandime pa lonjezani la Mulungu kudzera mu kusakhulupirira, koma anali wolimba, akudziwa kuti anamulandira iye munga m’modzi wochokera kwa akufa; wotsimikizika kwathunthu kuti ngati Mulungu ananena choncho, kuti iye achite izo, Iye akanakhoza kumuukitsa iye kwa akufa.” Ameneyo anali Abrahamu, ndipo imeneyo ndi Mbewu yake ya pambuyo pake. Ngati imeneyo inali mbewu yachibadwa, kodi Mbewu yachifumu ikuyenera kukhala motani? Sanadzandime! Chimene Mulungu wanena, Mulungu adzachichita. Podziwa izo, iye anatsimikizika kwathunthu; kuti chimene Mulungu analonjeza, Mulungu anali wokhoza kuchichita.

<sup>167</sup> Ananola mpeniwo; maso aang’ono akuda a Isaki akuwuyang’ana mpeni wakuthwa wawukuluwo pamene iwo unli kudutsa pa mwala. Anafikira kumbuyo; anaponyera mmbuyo tsitsi lopiringizika pa nkho pe pake, anakokera chibwano chake chaching’ono mmbuyo. Anadzuka, ndipo misozi ikuyenderera pansi pa nkho pe yake munga choncho. Akudziwa, ndipo iye sanadzandime pa lonjezo la Mulungu! Anakweza dzanja lake kuti aponye mpeni pakhosi la mwana wake yemwe.

<sup>168</sup> Ndipo pamene iye anatero, liwu la Mulungu linafuula, ndipo linagwira dzanja lake, linati, “Abrahamu! Abrahamu, letsa dzanja lako! Ndadziwa tsopano kuti iwe ukundikonda Ine.” Kodi Iye amachita chiyani? Amapereka umboni kwa Mbewu ya Abrahamu, ya pambuyo pake. “Letsa dzanja lako, usamupweteke mwana yu! Ine ndikudziwa kuti iwe umandikonda Ine.”

<sup>169</sup> Ndipo pa nthawi imeneyo, Abrahamu anamva chinachake kumbuyo kwake. Ndipo iye anayang’ana, ndipo apo panali nkho sa (ndiyo nkho sa yamphongo) yogwidwa ndi nyanga zake mu udzu ndi tchire. Ndipo Abrahamu anapita ndipo anakaitenga nkho sa yamphongoyo ndipo anayipha iyo, mmalo mwa mwana wake.

<sup>170</sup> Kodi nkho sa yamphongoyo inachokera kuti? Iye ali mailosi handiredere kuchokera ku chitukuko. Bwanji, zilombo za mtchire zikanayipha iyo ngati iyo ikanakhala kumeneko. Ndithudi, iyo ndi—iyo ndi nyama yoweta. Kodi iyo inachokera kuti?

Ndipo, pambali pa izo, ndi pamwamba pa phiri, pamene sipamakhala udzu kapena madzi. Ndipo Abrahamu anatola miyala mozungulira, pamene iyo inali, kuti apange guwa. Kodi iyo inachokera kuti? Sanali masomphenya; iyo inakhetsa magazi. Masomphenya samakhetsa magazi. Aleluya! Yehova-Yire anali atadzzipatsa Yekha nsembe!

<sup>171</sup> Pamene Mulungu atengedwa pa Mawu Ake, Iye amatha kupereka chirichonse chimene Iye akuchisowa. Mulungu, Yehova-Yire, akanali Yehova-Yire usikuuno. Iye ali ndi Nsembe yoperekedwa kale. Iye ali ndi Mpingo woperekedwa. Iye ali ndi Mtumiki woperekedwa, Mzimu Woyera. Iye ali pano tsopano, Yehova-Yire. Ambuyez wadzzipatsa Yekha Baibulo, Mzimu, Mpingo, Uthenga, Mtumiki. Ndipo ora liri pano tsopano kuti Mpingo ukwatulidwe ndi kutengeredwera kwawo. Yehova-Yire apereka njira kuti awutengere Mpingo umenewo kuwuchotsa mu dziko lino, posintha matupi athu ofooka awa, ndi kuwatengera iwo mmwamba ku Ulemelero. Yehova-Yire! Kodi zidzachitika chotani mu tsiku lamakono monga limene ife tikukhalamoli, kuti zinthu izi zidzakhalepo?

<sup>172</sup> Billy, mwana wanga wamwamuna, kulikonse kumene iye amakhala, ndi ine, tinali ku India posachedwapa. Ndipo ine ndinatenga pepala... Pamene ine ndinatsika ngalawayo, masauzande anali atayima pamenepo ndi nkhatu zamaluwa pafupi ndi milu. Pamene ife tinafika ku Taj Motel, iwo anali ndi pepala liri pamenepo, mu Chingerezi. Ndipo ine ndinaqona chidutswa chachikulu mmenemo, chinati, "Icho chikuyenera kukhala chizindikiro kuti chivomezi chatha." Kodi vuto linali chiyani? Chabwino, pafupifupi masiku atatu kapena anayi chivomezi chachikulu chisanachitike monga inu munawerenga, mbalame zazing'ono zonse zimene zinkakhala mmatanthwe...

<sup>173</sup> Ku India, alibe mipanda monga momwe tiri nayo mu California, United States. Iwo amapanga mipanda yawo ndi miyala imene amayitola. Ndipo mbalame zazing'onozo zimamanga chisa chawo mmenemo. Iwo amamanga nsanja zazikulu, ndipo mbalame zimamanga zisa zawo mmenemo. Ndipo mbalame zazing'ono zonse, masiku angapo chivomezi chisanafike, zinawulukira kuchoka ku makomawo. Ndipo nthawi ya kumadzulo kapena... Pakati pa tsiku, pamene kunatentha, nkhosha ndi ng'ombe zimakhoza kuima pansa pa mthunzi wa khoma ndi nsanjayo, kuti zisawotchedwe ndi dzuwa.

<sup>174</sup> Koma kwa masiku awiri, ng'ombe ndi nkhosha sizinabwere pakhomapo. Izo zinayima pakati pa bwalo ndipo zinatsamirana wina ndi mzake, ngati chitonthozo. Kenako chivomezi chinabwera, chinadzagwedezera makoma amenewo pansa. Ndipo kenako mbalame zazing'ono zinayamba kubwerera, ng'ombe kuchoka kuthengo. Chinali chiyani chimenecho? Mulungu yemweyo amene ankayitana nkhosha ndi ng'ombe, ndi mbalame, kulowa mu chombo, anawonetsera kuti Iye ndi

Mulungu yemweyo lero amene angathe kuziyitanira kutali nyama Zake.

<sup>175</sup> Ndipo ngati Iye angatsogolere nyama mwa kununkhiza, ndi mochuluka bwanji momwe Mpingo wa Mulungu ukuyenera kuchoka ku makoma aakulu opangidwa ndi anthu awa ndi ziphunzitso za mipingo. Babulo adzagwa, ena a masiku awa. Yehova-Yire wadzipezera Iyemwini Malo Opumulirako kwa inu. Ulukirani kutali kuchoka ku nsanja zapadziko lapansi!

<sup>176</sup> Ulukirani kutali kuchoka ku kukongola kwa Hollywood! Mpingo ikuyesetsa kuwanyoza iwo, kuwala. Uthenga sumawala. Hollywood amawala; Uthenga umanyezimira. Hollywood imawala ndi kukongola. Mpingo waukulu umawala ndi maphunziro. Ndipo Mpingo wa Mulungu wamoyo umayaka ndi kudzichepetsa ndi kukoma, ndi Mzimu Woyera. Pali kusiyana kwakukulu pakati pa kuwala ndi kunyezimira.

<sup>177</sup> Iye ali pano tsopano. Yehova-Yire wadzipezera Iyemwini. “Mulungu ndi wokhoza mwa miyala iyi kuwukitsa ana kwa Abrahamu.” Ngati zipembedzo sizivomereza Izo, Mulungu akhoza kuwabweretsa ana Ake kuchokera mmisewu, achiwerewere kuchokera mnyumba za alendo. Iye akhoza kudzutsa chirichonse chimene Iye akufuna. Koma ngati Mulungu wapereka Uthenga, pali winawake penapake woti alandire Iwo. Yehova-Yire! Ambuye adzipezera Iyemwini Uthenga. Ambuye adzipezera Iyemwini Mtumiki. Ambuye adzipezera Iyemwini, mwa njira ya Iye Mwini, zizindikiro ku Mpingo; osati kujowina, kulemba maina anu pa mabuku.

<sup>178</sup> Ife timamva zochuluka lero za zisankho, zisankho zochuluka. Nzaubwino wANJI kuwunjika miyala ngati ulibe womanga miyala pamenepo woti ayidule iyo ndi kuyipanga iyo kukhala ana aamuna ndi aakazi a Mulungu? Nchaubwino wANJI kukhala ndi zipembedzo zazikulu zomangidwa ndi masauzande, ngati winawake mulibemo mmenemo wokhala ndi Lupanga lakuthwa konsekonse la Mulungu kuti awawumbe iwo kukhala ana enieni a Mulungu? Akhoza kuwasiya iwo kunja kumene iwo ali. Amen. Mulungu (osati Methodist, osati monga Baptisti, Katolika), Mulungu wadzipezera Iyemwini Mpeni kuti awumbe ana a Mulungu, ana aamuna a Mulungu. Amen. *Yehova-Yire*, “Ambuye wadzipezera Iyemwini.” Ndipo Iye watero! Mukhulupirireni Iye, ndipo mukhale moyo.

Tiyeni tiweramitse mitu yathu mphindi chabe.

<sup>179</sup> Mulungu Wachisomo, Mulungu wamoyo nthawizonse, tichitireni ife chifundo tsopano, ndipo perekani kwa ife za chisomo Chanu. Ndife osayenera, Atate, chirichonse chimene Inu mungatichitire ife. Koma ife sitimavomereza kuti ndife oyenera, koma tikungomvera kuyitana kuchokera kwa Mulungu. Ife tikupemphera, Atate, kuti Inu mutiwumbe ife usikuuno kukhala miyala imene iti ikwanire mu Kachisi

wa Mulungu, chifukwa cha Kudza kwakukulu kwa Ambuye Yesu ku Kachisi Wake. Perekani izi, Atate. Tikhululukireni ife ochimwa zolephera zathu. Muwululire kwa ife Mawu Anu. Muwonetsere kwa ife Njira yoti tiziyendamo. Tiphunzitseni ife, O Atate Mulungu. Mulole ife tilandire Iwo. Ndipo ngati izo ziri zotsutsana ndi Mawu, ife tikudziwa kuti ndi mphunzitsi wolakwika. Mzimu Woyera ndi mphunzitsi wathu. Iye analemba Mawu, ndipo Iye sakanaphunzitsa chirichonse koma Mawu. Ndipo ife tikupemphera kuti Iye awonetsere izo kwa ife usikuuno, mu mtima mwathu. Perekani izi, Mulungu.

<sup>180</sup> Tsopano ndi mitu yathu yoweramitsidwa, maso athu otsekedwa. Chisomo cha Mulungu chikhale pa ife, ndiro pemphero langa lodzichepetsa ndi lowona mtima. Mungokhulupirira tsopano. Musakayikire.

<sup>181</sup> Kodi alipo aliyense mnyumba muno, chimene ine ndikudziwa kuti alipo, amuna ndi akazi amene sakumudziwa Iye, sanalandirepo konse Nsembe Yake yoperekedwa, Ambuye Yesu, ngati Mpulumutsi wanu? Inu simukumudziwa Iye? Inu mukhoza kuganiza mwaluntha kuti mumamudziwa. Koma munthu sangamuwone Mulungu mpaka atabadwa mwatsopano. *Kuwona* sikutanthauza... Sumawona ndi maso ako; iwe umayang'ana ndi maso ako. *Kuwona* ndi "kumvetisa." Inu umayang'ana pa Iwo, ndi kuti, "Ine sindikuchiwona icho," iwe ukutanthauza iwe "sukuzimvetisa izo." Inu simudzadziwa konse zimene tikuzikambazi mpaka mutabadwa mwatsopano. Inu simunakhalepo ndi chokuchitikirani chimenecho? Ndi mitu yanu yoweramitsidwa tsopano, ndi maso anu otsekedwa, kodi mungakweze dzanja lanu, ndi kuti, "M'bale Branham, ndikumbukireni ine mu pemphero usikuuno. Ine ndikukhulupirira kuti ife tikulandira Uthenga wathu wotsiriza. Tsiku likupita mofulumira. Ndipo ine ndikuona kuti chimene inu mwanena mu Baibulo ndi choona, chifukwa ine ndawerengapo Baibulo. Ine ndikukhulupirira kuti ndi ora limene ife tikuyenera kubwera tsopano. Ndipo, kwa ine, ine ndikupanga kuyima kwanga tsopano kwa Khristu?"

<sup>182</sup> Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu. Mmwamba mu khonde, manja! Mungokweza dzanja lanu, ndikuti, "Kwa ine, monga Yoswa anati, 'Kwa ine ndi nyumba yanga, tidzatumikira Ambuye.'" Chabwino, winawake? Ine ndikungodikirira. Mulungu akudalitseni inu kumbuyo uko. Ine ndikuwona dzanja lanu. Mulungu akudalitseni inu pamwamba apo. Mulungu akudalitseni inu. Iye akukuwonani inu. Mmwamba umo pa khonde, Mulungu akudalitseni inu pamwamba apo, bwana; chinthu chachikulu kwambiri chimene inu munachitapo mmoyo mwanu. Pakhonde lapakati pomwe, winawake kweza dzanja lako pamenepo. Mwinamwake ine



sindinawone dzanja mmenemo, mwina...Winawake mu khonde lapakati pamwamba? Kwezani dzanja lanu, ndi kuti, “M’bale Branham, kwa ine, ndine...ine ndikufuna kuti ndizimutumikira Iye. Ine—Ndine woona mtima.” Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu. Mulungu adalitse mwamuna wamng’onyo. Pakhonde kumanja, wina akweze dzanja lake pamenepo, ndi kuti, “M’bale Branham, ine, kwa ine, ine ndikudziwa izo nzoona. Ine...Ine sindikumudziwa Mulungu, koma ndikufuna kumudziwa Iye. Ndikufuna kukhala wotsimikiza. Ine ndikuwona kuti sindingakwanitse kutenga mwayi. Ine sindingakhoze konse kubwereranso.”

183 “Kumene mtengo umatsamira, ndi momwe iwo umagwera,” Malemba amatero. Musagwere mu njira imene ili yolakwika. Mukhoza kukonza izo usikuuno. Kumbukirani, pokhapokha ngati pali Muyaya, ndipo izo sizinachite kuyamba ndipo sizidzatha konse, koma inu mumakhala gawo la izo, inu mudzazunzika kapena mudzakhala mu chisangalalo. Inu mukudziwa bwanji kuti mukhala moyo mpaka mukafika kwanu?

Inu mukuti, “Ndine wamng’ono kwambiri.”

184 Ine ndangolandira kumene uthenga kanthawi kapitako. Dona wamng’ono kumbuyo ku dziko langa, anangotembenuza misewu molakwika, anayamba kusuta ndudu. Iye anali atauzidwa za Mulungu, koma iye sanamvere. Usinkhu wa zaka sikisitini zakubadwa, iye ankachokera kwa iye...ayi, usinkhu wa zaka eyitini zakubadwa, anali atangomaliza maphunziro a kusekondare. Ndipo anauzidwa, kuyesera kuti azichita zabwino. Koma iye anayamba ndi gulu lolakwika, mphezi inamupha iye nthawi yomweyo.

185 Posachedwapa, bambo wachikuda mu Shreveport anaimirira ndipo anati, “Palibe chinthu ngati Mulungu.” Anangochitira mwano, anati, “Iwo sikanthu koma gulu la oyera odzigudubuzwa.” Mphezi inamupha iye. Iwo anamutengera iye kumanda. Ndipo pamene ankamuyika munthu ameneyo, apo panabwera kamtambo kakang’ono, ndipo mphezi inakantha bokosilo ndipo inamuponyera iye kunja kwa bokosilo.

186 Yehova Mulungu amakwiya. Ine ndikudziwa kuti Iye ndi Mulungu wabwino, koma Iye ndi Mulungu wachiweruzo, nayenso. Iye akuyang’anabe, Iye akudziwa.

187 Ngati mulibe Mulungu, kwezani dzanja lanu, ndikuti, “Ndikumbukireni ine, M’bale Branham, pamene mukupemphera.” Mulungu akudalitseni inu, dona. Mulungu akudalitse iwe, mwana. Uko nkulondola, kazibwerani patsogolo. Mulungu akudalitseni inu. Uko nkulondola, mnyamata. Mulungu akudalitseni inu kumbuyo uko. Inu mumupemphe Mulungu Wamphamvuzonse.

<sup>188</sup> Atate athu Akumwamba, tsopano Inu mwawawona iwo. Inu mukudziwa pali manja twente kapena sarte amene ali mmwamba, amene iwo akukufunani Inu kuti mukhale Mpulumutsi wawo. Mulungu, perekani izi pakali pano. Ine ndikuwapatsa iwo Mawu awa. Inu munati, Inumwini, “Iye amene amva Mawu Anga.” Ine ndachita mopambana momwe ine ndikanathera ndi Iwo, Ambuye. “Iye amene amva Mawu Anga ndi kukhulupirira pa Iye amene anandituma Ine, ali nawo Moyo Wamuyaya, ndipo sadzabwera ku chiweruzo, koma wadutsa kuchokera ku imfa kupita ku Moyo.” Ndi chinthu chodabwitsa bwanji, kuganiza zimenezo! Ngati mitima yodzipereka kuseri kwa manja amenewo, kwenikweni imatanthauza zimenezo, chinachake changochitika kumene. Tsopano Inu munati, “Iye amene adzandivomereza Ine pamaso pa anthu, iye Ine ndidzamuvomereza pamaso pa Atate Anga ndi Angelo oyera.” Mulole iwo adziwe kuti Inu muli pano, Ambuye. Ine ndikupemphera kuti Inu mupereke izo. Timvereni ife. Ndife antchito Anu, Ambuye. Mu Dzina la Yesu.

<sup>189</sup> Chabwino, kwezani mutu wanu. Inu mukukhulupirira kuti Iye ndi Yehova-Yire? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Kodi inu mukukhulupirira kuti ife tiri mmasiku monga zinaliri mmasiku a Loti? [“Ameni.”] Masiku a Nowa? [“Ameni.”] Mukukumbukira Uthenga wotsiriza?

<sup>190</sup> Kodi alipo winawake pano kwa nthawi yawo yoyamba? Kwezani dzanja lanu. Ambiri! Ine ndikuganiza M’bale Borders wakufotokozerani inu. Inu mwamvapo za msonkhano kale, chimene chimachitika. Kwezani manja anu, ngati inu mwatero; ngati simunaziwonapo izo, munangomva izo. Chabwino. Tsopano ndine mlendo kwa anthu pano.

<sup>191</sup> Ena a anthu inu muli ndi vuto, pempherani kwa Mulungu, ndikuti, “Mulungu, ndichitireni chifundo, ine ndikudwala. M’bale Branham sakundidziwa ine. Koma ndikumva kuti Inu ndi Wansembe Wamkulu amene angathe kukhudzidwa ndi kumverera kwa zowawa zathu.” Ndi angati akudziwa zimenezo? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. “Ndipo Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.” Inu mukudziwa zimenezo? [“Ameni.”] Chabwino, tsopano, ngati Iye ali Wamkulu Wansembe yemweyo, kodi Iye angachite chotani ngati inu mukanamukhudza Iye? Momwemo mmene Iye anachitira pamene mkazi wa vuto la magari anamukhudza Iye. Iye anatembenuka ndipo anamuuzza iye chimene vuto lake la magari linali, ndipo anamuuzza iye kuti chikhulupiriro chake chinamupulumutsa iye. Ndi kulondola uko? Iye ali Mmodzi yemweyo usikuuno, ngati inu mungamukhulupirire Iye mwanjira yomweyo imene Iye anali nthawi imeneyo. Kodi inu mukumukhulupirira Iye mwanjira imeneyo?

<sup>192</sup> Tsopano inu muyang’ane mbali iyi, kwa ine. Monga Petro ndi Yohane ananena pa Chipata Chokongola, “Yang’anani pa

ife.” Izo sizinali “kuyang’ana pa iwo” pa chirichonse, koma, “kuyang’ana chimene iwo ankanena.”

193 Tiyeni tiyambire *apa* penapake. Yang’anani mbali iyi, ndipo mukhulupirire ndi mtima wanu wonse. Ndikuti, “Ambuye Yesu, ine ndikukukhulupirirani Inu, ndipo ine ndikufuna ndikhudze chovala Chanu. Inu muyankhule kwa M’bale Branham, ndipo mumulole iye adziwe chimene vuto langa liri. Ine ndikukhulupirirani Inu ngati Inu mungachite izo.” Kodi inu mungachite zimenezo?

194 Tsopano apa pali chinthu cholimba mtima. Kodi ine ndingayerekeze bwanji kuchita chinthu ngati chimenecho? Ine ndingakhale chinachake cholakwika ndi ine kupanga chitsutso chotercho. Ine ndawitsapo izo pamaso pa pafupifupi theka la millioni, panthawi imodzi, sindinkatha nkomwe kuyankhula chinenero chawo. Koma Iye sanandikhumudwitse ine. Chifukwa chiyani? Iye analonjeza izo! Ano ndi masiku otsiriza, ndipo Iye analonjeza izi, ndipo ndi izi apa.

195 Ine ndikudziwa, abwenzi, mwakhala ndi zambiri zoti zikupwetekeni. Mwakhhalapo ndi zokopera zachithupi zambiri. Koma ndiloleni ine ndinene chinthu chimodzi kwa inu, osati kwa phindu langa, koma kuti inu mupindule. Iwo nthawizonse amakhala nazo izo. Koma Mulungu sanakhalepo ndi awiri padziko lapansi nthawi imodzi, sanateropo. Koma ingokumbukirani, pali zokopera zambiri, koma alipo Mulungu weniweni. Ulipo Mzimu Woyera weniweni. Ulipo Uthenga weniweni wa Mulungu, ndipo umenewo ndi wakuti Yesu Khristu anafera ochimwa, anaukanso kwa akufa, ndipo wabwereranso mu Umunthu wa Mzimu Woyera, kuti adzachite ntchito yomweyo mu Mpingo imene Iye anachita pamene Iye anali kuno.

196 Tsopano, kodi Mawu a Mulungu samanena izi? Mu Ahebri, Iwo anati, mutu wa 4, Baibulo linanena kuti, “Mawu a Mulungu ndi akuthwa, amphamvu kwambiri kuposa lupanga lakuthwa konsekonse, odula pakati,” ndiko kudula ziwiri zonse kubwera ndi kupita, “ndipo ngakhale mmafuta amu fupa, ndi Wozindikira za mmalingaliro ndi zokhumba za mtima.” Nkulondola uko?

197 Ndi chifukwa chake Yesu ankakhoza kuyima pamaso pa omvetsera ndi kuwauza iwo. Afarisi aja anati, “Iye ndi Belezebule,” Yesu anatembenuka, iwo sanayankhule izo mokweza, koma Iye anawauza iwo. Ndi chifukwa chake Iye anakhoza kumuza mkaziyo za vuto lake la magari, anamuza mkaziyo kuti anali ndi amuna, ndipo pamene iye anachita izo, kenako Iye anati, “Bwanji, ndicho chizindikiro cha Mesiya!”

198 Inu mwaona tsopano kubwererako, kuwonekera kwa Mesiya pakati pa anthu. Ndi Mzimu Woyera ukukonzekeretsa Mpingo.

199 Ine ndikufuna inu mutembenuze mutu wanu. Mumuwone mkazi wamng’ono uyo akufikira apo, akudzuka, wakhala pansa

pomwe apa? Mukuona Kuwala uko pa iye? Iye akuvutika ndi kuthamanga kwa magazi. Uko nkulondola. Wavala diresi ya buluu, kukhala ngati wavala magalasi pa nkhope yake. Kwa sekondi yomaliza, kapena ziwiri, iye wakhala akumva kutentha kwachirendo pomuzungulira iye. Izo nzoona. Tsopano kuthamanga kwa magazi kwanu, kumene kwakhala kukusautsani inu kwambiri, kwakuchokerani inu. Inu mukuvomereza zimenezo? Kwezani mmwamba dzanja lanu ngati inu mukutero.

<sup>200</sup> Kodi iye anakhudza chiyani? Wansembe Wamkulu. Tsopano kazipitani, mufunseni donayo. Ine sindinayambe ndamuwonapo iye mmoyo wanga. Ine sindikudziwa chinthu chimodzi chokhudza mkaziyo; koma, izo nzoona. Ine ndimayang'ana Kuwala kumeneko pamene Iko kumasuntha kudutsa omvetsera awa, kunapita uko ndi kubwerera, Kuwala koyaka.

<sup>201</sup> Kodi inu mukukhulupirira? Nyamakazi, vuto la chikhodzodzo, zovuta, manjenje, kufooka. Uko nkulondola. Sindinu wochokera kuno. Malo aang'ono otchedwa West Point. Uko nkulondola. Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu akhoza kundiuza ine yemwe inu muli? Abiti Hardwick. Uko nkulondola. Ngati izo ziri zoona, imirirani pa mapazi anu. Izo zakusiyani inu. Yesu Khristu wakuchiritsani inu.

<sup>202</sup> Kodi inu mukukhulupirira? [Osonkhana akuti, "Inde."—Mkonzi]. Anthu akuyang'ana mmbuyo, kwa izo. Apa pakhala donayo pomwe apa. Penyani, Kuwala kumeneko kukadali pa iye. Kodi inu simukukuwona Iko? Ndi Uku apa. Penyani.

<sup>203</sup> Ndi Uku apo, ndi bambo uyo wakhala apoyo akundiyang'ana ine. Nyamakazi. Akukhulupirira ndi mtima wake wonse, Mulungu akuchiritsani inu, bwana, inunso. Ndife alendo kwa wina ndi mzake, koma osati kwa Mulungu.

<sup>204</sup> Dona uyu kumbuyo komwe kuno, akuvutika ndi mutu. Mulungu, musamulole iye aphonye izo. O Mulungu, chonde. Abiti Morton, khulupirirani pa Ambuye Yesu Khristu. Iye anakuchiritsani inu ku mutu umenewo. Mwaona, Iye sakanamulola iye kuti adutse. Ine ndikufuna ndikufunseni inu chinachake. Usiku watha pamene ndinayankhala ndi winawake mchiphindamo za mutu wawo, inu munali ndi kumverera kwachilendo kwenikweni, ndipo inu mumadabwa ngati ameneyo anali inu, kapena ayi. Si kulondola uko? Kwezani mmwamba dzanja lanu. Ine sindikuwerenga malingaliro anu, koma ndikukuuzani inu chimene inu mwakhala mukuganiza. Uko nkulondola. Lero Iye amafuna kutsimikiza kuti ndi inuyo. Iko kukusiyani inu tsopano, chikhulupiriro chanu chakupulumutsani inu. Aleluya.

<sup>205</sup> Tayang'anani pa dona uyu wakhala apa, wavala diresi ya mandalasi. Kodi inu muli ndi khadi la pemphero, dona? Yang'ana lakolo. Kodi ukukhulupirira kuti kuphulikako kukusiyana iwe, iwe

ukhala bwino? Iwe ukutero? Kweza mmwamba dzanja lako ngati icho ndi chimene chiri chokuvuta iwe. Chabwino. Khulupirira ndi mtima wako wonse ndipo uchiritsidwa. Mukuona chimene chiri kwa ine?

<sup>206</sup> Dona kumbuyo kwa iye, anakweza mmwamba dzanja lake, ndi pang’ono. . . ayi, wachiwiri kumbuyo uko, wavala diresi laling’ono lowoneka la girini, akuvutika ndi vuto la mtima. Inde. Kodi iwe ukukhulupirira kuti Mulungu akuchiritsa iwe? Izo ndi zabwino, zopambana. Iye atero ngati ungakhulupirire izo.

<sup>207</sup> Dona, wachiwiri kuchokera kwa inu, Akazi a Dillman apo. Ngati inu mukukhulupirira kuti Mulungu akuchizani inu ku vuto la mmimba ilo. Akazi a Dillman, khulupirirani, ndipo inu mukhala mimba yanu. Ndi mimba yamanjenje. Izo zakhala ndi inu kwa nthawi yayitali, makamaka kuyambira pamene kusinthika kwa thupi kunakhala pa inu. Inu mwakhalapo ndi zinthu zambiri zimene zimakubweretserani inu mavuto ochuluka, koma zonse zatha tsopano. Ngati zinthu zimenezo ziri zoono, ingogwedezeni dzanja lanu kwa anthu, kuti iwo akhoze kuwona. Ngati ndine mlendo kwa inu, pitirizani kugwedeza dzanja lanulo. Yesu Khristu wakuchiritsani inu.

<sup>208</sup> Kodi inu mukukhulupirira? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Ndi chiyani chimenecho? Yehova-Yire, Ambuye amadzipezera Yekha Nsembe! Tsopano omvetsera onse akukhala ngati sakuwoneka kwa ine. Yehova-Yire wapereka Nsembe kwa aliyense wa inu. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo?

<sup>209</sup> Tsopano inu pano amene munakweza mmwamba dzanja lanu, bwerani kuno ndipo mudzayime apa miniti yokha. Kodi inu muchita zimenezo? Yehova-Yire wapereka Nsembe. Inu munakweza dzanja lanu, kuti inu mukukhulupirira izo. Inu mwaona apa, ndipo mukudziwa. Zosatheka. . . Ndi Chinachake! Tayang’anani pa anthu awa, ndi angati amene ayitanidwa. Ine sindikudziwa tsopano. Mwinamwake seveni, eyiti kapena teni, chirichonse chimene icho chinali, amene ayitanidwa. Izo zikhoza kumangopitirirabe. Koma pamene ine ndiri ndi mphamvu, ine ndikufuna kuti inu mbwere, mudzamulandire Khristu ngati Mpulumutsi wanu. Kodi inu muimirira tsopano ndi kubwera, pamene ife tikuyimba, “Ndikubwera, Ambuye, ndikubwera tsopano kwa Inu”? Kodi inu mungadzuke tsopano ndi kubwera kuno, inu amene munakweza dzanja lanu kanthawi kapitako? Ndi kudzayima mozungulira guwa pano, ndi kudzawonetsera kuti inu simukuchita manyazi ndi Khristu. Inu muli mu Kukhalapo Kwake. Bwerani tsopano, ndipo mutsimikizire kwa anthu kuti mumatanthauza zimenezo, kuti inu mukufuna kukumbukiridwa ndi Mulungu, ndipo mwamulandira Iye ngati Mpulumutsi wanu. Kazibwerani tsopano, pamene ife tonse tikuyimirira ndi kuyimba.

Ndikubwera, Ambuye!

Ndikubwera tsopano kwa Inu!  
 Ndisambitseni, ndiyeretseni mu Magazi  
 Amene anawukha kuchokera pa Kalvare.

<sup>210</sup> Kazibwerani tsopano, kazibwerani kumusi kuno komwe. Ife tipemphera. Simukakhala konse pafupi ndi Iye mukachokapo.

Ndikubwera tsopano kwa Inu!  
 Ndisambitseni, ndiyeretseni ine . . .

<sup>211</sup> Bwerani pansi kuchokera pakhonde. Uko nkulondola. Kazibwerani pansi pano, dzaimeni pomwe apa. Mukhale . . . Tsopano, Iye anati, “Ngati mudzandivomereza Ine pamaso pa anthu, iye Ine ndidzamuvomereza pamaso pa Atate Anga. Koma ngati mukuchita manyazi ndi Ine, Ine ndidzakuchitirani inu manyazi,” kumbukirani, Baibulo, kuyambira ku Genesis mpaka ku Chivumbulutso. Kazibwerani tsopano, achichepere ndi aakulu. Kodi inu mubwera? Membala wa mpingo, kapena ayi, kazibwerani tsopano. Kodi inu mutero? Mulandireni Khristu pamene inu muli mu Kukhalapo Kwake.

Ndikubwera, Ambuye!  
 Ndikubwera tsopano kwa Inu!  
 Ndisambitseni, ndiyeretseni mu Magazi  
 Amene anawukha kuchokera pa Kalvare.

<sup>212</sup> Muzingopitiriza, kuyimba. [M’bale Branham akung’ung’udza, *Ndamva Liwu Lanu Lolandira*—Mkonzi].

<sup>213</sup> Mvetserani. Kodi inu mukundikhulupirira ine kuti ndine mneneri Wake? Ine sindinavomerezepo zimenezo kale. Ine ndikukhulupirira kuti ndayima ndi anthu amene amamvetsetsa ndi kudziwa chimene ine ndikuyesera kubweretsa kwa inu. Muli anthu muno amene akudzinenera Chikristu, akuyenera kukhala pomwe *pano*. Bwerani, inu simutero? Ndiloleni ine ndikufunseni inu, kodi mudzachita konse chotani? Inu simudzalandira konse chizindikiro china. Ichi ndi Chimenecho. PAKUTI ATERO AMBUYE. Kodi mneneri wa Mulungu anganene mawu ngati amenewo ngati iwo si owona? Inu mukulandira chizindikiro chanu chachikulu, ndi chizindikiro chanu chotsiriza, kuwonekera kwa Khristu kusanachitike. Bwerani! Chifukwa chimene ine ndikunenera zinthu izi, ine sindinanenepo izi mu msonkhanu wina uliwonse, Ine ndikumverera kuti pomwe pano pali mwayi woti chinachake chichitike. Ndi chifukwa chake ndikunena momwe ndikuneneramu. Ine ndikukhulupirira kuti inu mukumvetsa. Inu simungapite uko, kumakapanga mtundu wina wachipembedzo, kumati, “M’bale Branham ndi mulungu,” kapena chinachake chonga icho. Inu mukumvetsa zimene ine ndikuzikambazi. Bwerani tsopano. Kazibwerani. Ndiloleni ine ndikukakamizeni inu, mu Dzina la Khristu. Kazibwerani!

<sup>214</sup> Inu amene simukudziwa pamene mwayima, simukutsimikiza za izo, waluntha basi, kapena mtundu wina wa

zomverera; inu mwalira, mwasisima, kapena inu–inu munali ndi mtundu wina wa kugirigisha. Inu musati mudzayesere kudzafika Pamenepo pa izo. Kumbukirani, ine ndikukuuzani inu mu Dzina la Ambuye, kuti inu mwatayika, mwatayika momvetsa chisoni, ndipo simukudziwa izo. Usatengere mwayi, mzanga. Ine ndikungofesa mbewu, ndi kumakoka ukonde. Mulungu amatenga zochulukazo. Ine sindikudziwa.

<sup>215</sup> Tiyeni tiweramitse mitu yathu, tiwone ngati Iye sandiuzza ine. [Mlongo akuyankhula mu lirime lina ndi kutanthauzira—Mkonzi]. Inu mukumva zimenezo.

Ndikubwera tsopano kwa Inu!

Fufuzani mtima wanu womwe.

Ndisambitseni, ndiyeretseni mu . . .

<sup>216</sup> Membala wa mpingo. Ngati ndikanati ndikuyima pamenepo, ndipo nkungokhala ndi chondichitikira chojowina mpingo . . . ? . . . Ine ndikanabwera kuno mwaliwiro basi mmene ndikanathera.

<sup>217</sup> Kumbukirani, Mzimu ukuchitira umboni kuti ife tiri kumapeto. Sayansi inati, “Kwatsala maminiti atatu kuti ifike pakati pa usiku.” Uthenga ndi Baibulo limati, “Ndi ichi apa, chinthu chotsiriza!” Chitsitsimutso chikutha. Khomo likutsekeka. Inu mudzakhala panja, mukugogoda, ndipo osatha kuti mulowe. Bwerani!

Mulungu akudalitse iwe, dona wamng’ono. Tsopano, kodi inu munaona zimenezo?

Ine ndikubwera, Ambuye!

Ndikubwera tsopano . . .

<sup>218</sup> Mulungu akudalitseni inu. Ndiko kulondola, bwana. Njira yake ndi imeneyo, bwerani kuno kuchokera pakhonde. Muzibwera mmizere.

<sup>219</sup> Mawu ake ndi awa, umboni wake ndi uwu. Ndi umenewo Mzimuwo, mboni ndi zimenezo. Ndipo apa anthu akubwera, kudzawonetsera kuti ife tiri pano ku nthawi yotsiriza.

Ndikubwera, Ambuye!

Ndikubwera tsopano kwa Inu!

Ndisambitseni, ndiyeretseni mu Magazi

Amene akuyenderera kuchokera pa Kalvare.

Ndikubwera, Ambuye!

<sup>220</sup> Kudikirira, kuyitana ena. “Osafuna kuti wina awonongeke; onse akhoze kubwera ku kulapa.” “Bwerani,” anati, “kwa Ine.”

<sup>221</sup> Ngati munali ndi kukayikira mmaganizo mwanu. Mukuyenera kukhala otsimikiza, amzanga. Chikhulupiriro ndi changwiro.

. . . kuchokera pa Kalvare.

. . . Ambuye!  
Ndikubwera tsopano ku . . .

<sup>222</sup> Ena, anthu fifite mpaka sevente-faivi asonkhana mozungulira. Tsopano bwerani. Aloleni ena onse amene akuyenera kubwera. Kugwira motalika pang'ono tsopano. Chifukwa, mawa zidzakhala pa machiritso Auzimu. Mzimu Woyera unayankhula ndi ine, kanthawi kapitako, "Usayitanire mzere umenewo. Itanira guwa." Ine ndimumvera Iye ndi kuchita momwe Iye wandiuzira ine. Ine ndikudziwa bwinoko kuposa kusachita izo.

Ndikubwera tsopano kwa Inu!  
Ndisambitseni, ndiyeretseni mu Magazi  
Amene anayenderera kuchokera pa Kalvare.

Ndi mitu yathu yoweramitsidwa tsopano, pamene ife tikuyembekezera.

<sup>223</sup> O Mulungu, mulole Mzimu Woyera uyenderere pa awa. Iwo amene akufuna kubwera kutsogolo pa guwa, kuwatsogolera anthu tsopano ku mdalitso. Ndipo—ndipo mulole Ambuye Mulungu apereke zimenezo. Mzimu wa Mulungu, ukuyankhula.

<sup>224</sup> Sunthirani mkati, sunthirani mkati. Bwerani pafupi tsopano, aliyense. "Solo iliyonse, yoponderezedwa ndi tchimo, pali chifundo ndi Ambuye." Bwerani tsopano. "Abwere pansu pa kusefukira koyeretsa, adzataye zoipa zawo zonse. Pali Kasupe wodzazidwa ndi Mwazi, wochokera mu mitsempha ya Emanuele." Mwaulemu.

<sup>225</sup> Mukumverera mtendere umenewo pa msonkhano tsopano? Kod ndi chiyani chimenecho? Ndi imfa, imfa kwa ochimwa. Tsopano othandizira muyende mozungulira ndi iwo tsopano. Ndi imfa, anthu awa akufa. Mabaibulo atuluka, iwo akufotokoza. Imfa ikupita mozungulira guwa, ndipo Moyo watsopano ubwera pambuyo pa imfayo.

Kuli kasupe wodzazidwa ndi Mwazi,  
Otengedwa kuchokera . . .

Oh, momwe mudzafunire kudzamva zimenezo tsiku lina, tsiku limene kugunda kwanu kudzasiya!

Ndipo ochimwa akaziponyera pansu pa  
kuyendererako,  
Ataya zoipa.  
Ataya zoipa,

Ndi zimenezotu, mnyamata wamng'ono. Adalitse mtima wako. Icho ndi chimene Iye amayembekezera.

Ndipo ochimwa akadziponyera pansu pa  
kusefukirako,  
Ataya zoipa.



226 Tsopano mulole Akhristu amene alangizidwa, asunthire kumtunda pamene ife tikuyimba ndime yotsatira. “Wakuba wakufa anakondwera kuwona Kasupe ameneyo mu tsiku lake; pamenepo ine, ngakhale woyipa ngati iye, nditsuka machimo anga onse.” Mulole anthu olangizawo tsopano abwere pafupi. Inu amene mulibe ubatizo wa Mzimu Woyera, yandikirani pafupi tsopano. Inu simukudziwa chimene Mulungu angachite tsopano mu miniti. Yendani mmwamba tsopano, pamene ife tikuyimba ndime yotsatira tsopano.

Wakuba pakufa anasangalala . . . (Mawu  
atawonetseredwa.)

Kasupe mu tsiku lake;

Oh, ziri bwino, tulukani tsopano. Bwerani pamene Madzi akuvutitsidwa.


. . . Ine, ndi woyipa monga iye,  
Mutsuke machimo anga onse.  
Mutsuke machimo anga onse,  
Mutsuke machimo anga onse;

227 Ndi zimenezotu, ogwira ntchito. Lowani momwemo. Onse amene akubwera tsopano ku Madzi ovutitsidwa. Bwerani komwe kuno.

. . . woyipa monga iye,  
Mutsuke machimo anga onse.

228 Tsopano inu amene mukufuna kuti mupemphere, yandikirani pafupi tsopano ndi kukonzekera. Ife tikhulupirira kuti Mulungu atero, azindikira ichi. Iye akuyenera kutero! Mulungu yemweyo amene akhoza kuzindikira lingaliro la mtima! Kumbukirani, Yesu anachita izo nthawi imodzi yokha mu mzinda. Koma Iye anati, “Zoposa izi inu, mudzazichita.” Mwaona, anatsimikizira Lemba Lake molondola! Sunthirani mkati tsopano. Tiyeni tonse tsopano tiwapempherere anthu awa amene ali pano. Munthu aliyense amene amadziwa kupemphera. Ndi Akhristu obadwa mwatsopano angati amene ali mnyumba muno? Kwezani mmwamba dzanja lanu. Tsopano tiyeni aliyense akweze manja athu ndi kupereka mathokoza chifukwa cha anthu awa.

229 Atate athu Akumwamba, ife tikupereka mathokoza kwa Inu chifukwa cha anthu awa. Iwo ndi Anu. Iwo akubwera, kudzapanga kuvomereza. Iwo akubwera kudzafa kwa iwoeni ndi kwa tchimo. Iwo akubwerera, ali zolengedwa zatsopano mwa Khristu.

230 Satana, wagonja nkhondoyo! Mulungu ndi Yehova-Yire! Ambuye wapereka Nsembe, wapereka anthu, wapereka kuitanira kuguwa, wapereka Uthenga, wapereka chisomo. Ndipo Satana wagonja nkhondoyo, mu Dzina la Yesu Khristu iye wagonja nkhondoyo! 

62-0707 Yehova-Yire #3  
Municipal Auditorium  
Grass Valley, California U.S.A.

CHICHEWA

©2024 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)